

M'BADWO WA MPINGO WA EFESO



Ambuye akudalitseni inu.

Aliyense mkati muno amene akuyendetsa a—a Dodge, Dodge yatsopano, nambala yake WX-2129, yaimitsidwa kutsidya kwa msewu uko? Asiya nyali zawo, nyali zazikulu ndi zonse, nzoyatsa. Ndipo ngati winawake ameneyo akuyendetsa galimoto imeneyo, bwanji, tulukani panja ndipo mukazimitse nyali zanu. Ili kumbali ya dzanja lakumanzere kwa msewu, kutsikira ku Eighth Street. Ine ndikulingalira kuti ndi nambala ya New Albany imeneyo, WX-2129. Dodge yofiira, Dodge yatsopano, ili pafupifupi pa '59, '60, kapena kwinakwake kumeneko. Ndipo ine sindikudziwa ngati muli winawake muno kapena winawake anali basi. . . akuchokera kwinakwake. Chabwino, izo zinali. Ndipo ndiye ndicho chinthu chabwino. Tsopano, ine sindinena kuti azimayi okha amene amaiwala zimenezo, chifukwa inenso ndimatero.

² Chabwino, ndithudi ndi chabwino kuti tabwereranso kachiwiri usikuuno mu msonkhano, ndi kudzakhala ndi nthawi yabwino iyi ya chiyanjano limodzi pozungulira Mawu. Kodi inu mukusangalala Nazo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi]. Oh, uko nkulondola, ife tikungokhala ndi yodabwitsa, nthawi yodabwitsa. Ndipo tsopano ife tikudalira kuti Mulungu atithandiza ife kuti tizipitirirabe.

³ Tsopano, mchimwene wanga anapita ndipo wakatenga bolodi yakuda apa, koma iyo ndi—ndi yayifupi kwambiri, iyo siikufikira mmwamba mokwanira. Chotero mawa, chabwino, ine ndiyesetsa kuti ndidzaikonze iyo pamwamba apa, ndikuisunthira iyo mmwamba ndikuipanga iyo chomwecho. . . Ine ndikufuna ndizijambula zinthu zina zosiyanasiyana zimene ine ndikufuna kuti ndizifotokoze, kuti inu mukhoze basi. . . ndipo basi kuchitira kuti inu mukhale otsimikiza kuti inu mukuzimvetsa Izo kwenikweni.

⁴ Panali. . . Dzulo usiku, kapena dzulo anali, mtsikana wanga wamng'ono, Sarah, anachita ngati mosangalatsa. Amake ndi ine tinali kuyang'ana pa pepala lake laling'ono; iye amatenga zolemba zanga. Ndipo anali atalemba zonse molondola basi, Yesaya ndi Mateyu ndi chirichonse. Ndipo kumapeto kwenikweni kwa—kwa pepala, iye anali “Ndi—ndi imfa. . . Manda alibenso chigonjetso chirichonse pamenepo, ndipo imfa mbola yake inali itazulidwapo.” Iye ndi wa pafupifupi usinkhu wa zaka seveni. Ndipo kenako iye mmalo moti ati “Revelation,” iye anati, “Bukhu la revolutions.” Chabwino, izi zikuwonetsa kuti iwo akumakhala ndi chidwi chofuna kupeza chinachake, mulimonse, sichoncho iwo? Ine

ndikuganiza mtsikana wamng'ono wa M'bale Collins, iye wakhala kumbuyo uko, ndipo iwo analemba (“Revolution”?), “Tsiku la revolutions,” M'bale Neville akutero. Iye akugwirizana naye iye. Ine ndikuganiza ife tonse timayenera kuchita zimenezo.

⁵ Chabwino, ife ndithudi tikukhala ndi nthawi yopambana. Mai, Ambuye akudalitsa. Ine ndinalowa umo kuti ndikawerenge mmawa uno, mchipinda, nditangokawasiya ana ku sukulu, ndipo ndinangotuluka kanthawi kapitako; ndikungokhala ndi nthawi yabwino. Dzulo usiku, ndinawerenga ngati mochedwerapo, nanenso.

⁶ Ndipo pafupifupi hafu-pasiti thuu mmawa anthu ena anabwera kuchokera kumpoto, iwo anatipeza ife... anadzandizutsa ine kuti ndimupempherere mtsikana wamng'ono amene anali akufa. Ndipo ine ndiri wotsimikiza Ambuye amulola iye kuti akhale bwino. Iwo anangobwera kumusi, njira yonse kuchokera ku Bedford, Indiana, kudzafunsa chopempha kuti mtsikana wamng'onoyo apemphereredwe pamenepo. Amuna awiri anali mu msonkhano usiku wathawu ndipo anayendetsa njira yonse chokwera uko, kenako nkumabwereranso akutsikira mmusi, kenako njira yonse amabwereranso. Mwinamwake usiku wonse amayendetsa. Ndipo chotero, ndi zabwino kudziwa kuti anthu ali ndi chidaliro chotere ndipo amakhulupirira Mulungu.

⁷ Oh, ndi tsiku lopambana limene ife tiri nkukhalamo. Ndipo ife tikuyembekezera tsopano, pa mibadwo ya mipingo iyi, kuti tingopeza zochulukira chulukira.

⁸ Tsopano ife tikuyesetsa kuti tiziyamba molawirira pang'ono usiku uliwonse, kuchitira kuti tizituluka molawirira. Inu mukuzikonda bwino zimenezo? Ndipo zimenezo zikuwalola anthu omwe ayenera kuti akagwire ntchito, akafike kunyumba kuti akakhoze kupita ku ntchito. Dzulo usiku ife tinatuluka pafupifupi maminiti faivi, maminiti teni itakwana naini, kapena osachepera ine ndinali nditamaliza. Ndipo chotero ndife okondwa kukhala ndi atumiki onse odzatichezera ife usikuuno. Ndipo ine—ine... M'bale Junior Jackson, M'bale Carpenter, ndi m'bale wathu wochokera ku tchalitchi kumeneko, ndi ena ambiri pa nsanja pano ndi kunja mu msonkhano.

⁹ Ndipo ine ndinauzidwa lero kuti mzanga wofunika kwambiri yemwe anali ndi ine mminda ya umishoni, M'bale ndi Mlongo Andrew ochokera kutali kwambiri ku China, anali mu msonkhano usiku watha. Inali nthawi yodabwitsa bwanji imene ife tinali nayo limodzi ku Jamaica chaka chathachi. Ife tinali ndi nthawi yopambana, ine ndinali uko ku nyumba yawo. Ndipo mai, ngati... Ine ndikudabwa ngati M'bale ndi Mlongo Andrew alipo usikuuno kuno mu—mu msonkhano? Nyumbayi sinamangidwe bwino basi, chotero... Eya, akhala kumbuyo komwe uko. Ine ndikudabwa ngati inu mungakhoze kukwanitsa

kuti muimirire pa mapazi anu, M'bale ndi Mlongo Andrew, mphindi chabe. Ambuye akudalitseni inu. Ndife okondwa kwambiri kukuwonani inu, M'bale ndi Mlongo Andrew. Ine ndinawaitana iwo kuti abwere chaka chatha pamene ine ndinali kumeneko.

¹⁰ Tsopano, sindikunena izi chifukwa chakuti ali pano (ine ndimati ndinene zambiri, koma ine sindinena izo tsopano), koma iwowo ndi omwe ine ndimawatcha amishonare enieni. Ngati iwo ati adzabwere mawa usiku, mudzawauze iwo kuti adzayankhule pano ife tisanalowe muno. Ine ndikufuna kuti inu mudzamve kwenikweni chimene munda ya umishoni imatanthauza, pamene iwo anali atabwerera mkati momwe kwambiri mpaka iwo analibe ngakhale chirichonse...Chabwino, iwo ali...Ine ndikuganiza kuti zinali zaka ndi zaka ndi zaka zimene iwo anali kumbuyo uko, ndipo iwo sanaiwone nkomwe galimoto kapena sitima, kapena china chirichonse, kwa zaka ndi zaka. Ndi momwe Mlongo amapangira mkate wawo kuchokera... Momwe iye amapangira iwo. Ndipo...Tsopano, ndiwo umishonare weniweni. M'bale Andrew anali ndi singano ndi ulusi ndipo iye anali dokotala, iye ankawasoka iwo onse akavulala. Ndipo ine ndikuganiza pamene mwana...ana akamabadwa, Mlongo Andrew mwinamwake amakhala mzamba ndipo M'bale Andrew dokotala. Iwo amangodalira pa iwowo.

¹¹ Ndiyeno pamene amishonare a...ochokera ku England, a Pentecostal Missions of England, amati iwo anali “atakalamba kwambiri kuti azibwerera kumunda,” (Ine ndingokuwuzani inu kuchuluka kwa momwe iwo aliri mamishonare, iwo samatenga mpando wophweka ndi kukakhala pansu) iwo amabwerera kumeneko okha okha, kubwerera ku Jamaica ndi kunja uko kukakhala amishonare tsopano. M'bale Fred Sothmann ndi ine pano tinali ndi mwayi wopita kunyumba kwawo ndi kukawayendera iwo, ndipo inali nthawi yosangalatsa bwanji imene iwo anatiwonetsera ife; mo—mokoma basi monga momwe Akhristu angakhalire. Ndipo ine ndikukuuzani inu, ine sindikunena izi kuti...Ine kulibwino kuti ndipereke kaduwa kakang'ono tsopano kuposa nkhatu iwo atapita. Ine ndikukuuzani inu, iwo ndi Akhristu ndithudi. Ndipo ine ndimamuza mkazi wanga kuti Mlongo Andrew anali mmodzi wa akazi Achikhristu okoma kwambiri, abwino kwambiri amene munthu akanakumanapo nawo. Iye ali basi... khalidwe lake linaumbidwa mwa Khristu, nalonso; ndi M'bale Andrew, nayenso. Chotero, ine ndikutsimikiza ngati inu nonse munawawona iwo omwe anangoimirira, Ine ndimafuna kuti mpingo wonse uno ugwirane nawo chanza ndi kuwamva iwo asanachoke.

¹² Tsopano, mawa, Ambuye akalola, bwanji, ndife...mawa usiku tikuyamba m'badwo wachiwiri uwu wa mpingo. Usikuuno ife tikuyamba m'badwo wa mpingo woyamba. Ine

ndikutsimikiza kuti Ambuye ali ndi dalitso lomwe atisungira ife.

¹³ Ndipo kumbukirani, monga ine ndinanenera kale, nthawizina pa zinthu izi ife tikhoza kusagwirizana tikakamba za—za momwe zimakhudzirana ndi fioloje. Ndipo madeti anga ambiri ndimawatenga kuchokera kwa olemba mbiriyakale enieni, omwe alibe chidwi kwenikweni ndi mbali iliyonse, iwo ankangolemba mfundo, chirichonse chomwe chinali, zomwe mipingo inkachita. Ndipo ine...Ndithudi, gawo Lauzimu la kutanthauzira, ine ndimayesetsa kuziika izo pamenepo inemwini, mopambana momwe ine ndikudziwira kutero. Ndipo nthawizina ngati ine ndiyankhula molimba pang'ono kapena mopupuluma monga choncho, ine sindimatanthauza izo mwanjira imeneyo. Aliyense akudziwa zimenezo, amene amandidziwa ine, kuti ine sindimatanthauza kuti ndichite zimenezo. Ine ndikungofuna...Koma kuti ndipange mfundo ikhazikike, inu...Zimakhala ngati kukhomerera msomali pa bolodi, ngati inu mungowusomeka iwo pamenepo, iwo sungagwire. Inu mumayenera kuti muwuyendetse iwo upite pansu ndi kuwugwiritsa iwo, kuwupangitsa iwo kuti ugwire. Ndipo ndizo zimene ine ndikuyesetsa kuti ndichite. Chotero sikuti ine ndikuyesa kuti ndizitsutsa, chifukwa ine ndimayankhulira zipembedzo zonse ndi zina zotero, chotero sizitero...kuti.

¹⁴ Ine nthawizonse ndimanena, monga kuika chizindikiro ng'ombe. Ine ndikukumbukira zaka zapitazo ine ndinali nditakhala tsiku lina pamene iwo anali...ankakadyetsera ku kasupe, ankazitenga ng'ombe kupita nazo ku thengo, ndipo ine ndinkathandizira kuyendetsa ng'ombezo zikamapita kumeneko, chimene iwo amachitcha mpanda wolowerera komwe a Hereford Association amakadyetserako ziweto mu—mu Troublesome River Valley. Ndipo ine ndinali nditakhala pamenepo mwendo wanga utapachikidwa pamwamba pa nyanga ya chishalo, ndikumuyang'ana woyang'anira pamene iye ankayang'anira ng'ombe izi zikudutsa kupyola mpanda wolowerera.

¹⁵ Tsopano, iwe umayenera kukhala ndi...pamenepo ndi pamene iwe ukupita ku malo a boma, ndipo iwe umayenera kukhala wokhoza kutolera tani ya udzu iwe usanakaziyike ng'ombe kumalo odyetserako ziweto. Ndipo malo owetera nyama aliwonse amakhala ndi msipu wambiri, ng'ombe zochulukwa kwambiri, ndiye izo zikhoza kumadya iwo.

¹⁶ Tsopano, izo zimadutsa kumeneko ndi mitundu yonse ya zizindikiro pa izo. Zina za izo zinali ndi “Bar X.” Bambo Grimes apafupi kumene ndi ife kumeneko anali ndi “Diamond T,” T kumapeto amodzi a diamondi. Uko kunali ameneyo “Lazy K,” kumutu kumene kwa Mtsinje wa Troublesome. Wathu unali “Turkey Track.” Pansi pathu pomwe panali “Tripod.”

Ndipo kunali mitundu yonse ya zizindikiro zomwe zimadutsa pachipata chimenecho.

¹⁷ Ndipo ine ndimawona kuti woyang'anirayo samasamala kwambiri zizindikiro zimenezo, iye samaziyang'ana nkomwe izo. Nthawiina izo zimakhala kumanzere kwa ng'ombe, chotero iye samatha kuwona chizindikirocho. Chotero izo—sikuti iye anali kuyang'ana chizindikirocho. Koma chinthu chimodzi chimene iye amakhala wotsimikiza, chinali kuti pasakhale ng'ombe yomwe itadutse pamenepo kupatula ikhale ndi cholemba cha mtundu wa magazi pa khutu lake. Iyo imayenera kukhala ya mtundu weniweni wa Hereford apo ayi iyo siimatha kupita ku nkhalango imeneyo. Chizindikirocho sichimapanga kusiyana kwakukulu, koma cholemba cha mtundu wa magazi. Ndipo ine ndikuganiza kuti ndi zomwe ziti zidzakhale pa chiweruzo. Izo sizidzakhala chizindikiro chomwe ife tavala, koma Iye adzafuna cholemba cha Magazi, “Pamene Ine ndidzawona Magazi, Ine ndidzadutsa pa inu.”

(Tsopano, kodi ine ndalakwa pang'ono, Gene, ndi choncho?) [M'bale Gene Goad akuti, “Maikrofoni *awa* akuphokosera.”—Mkonzi]. (Akuphokosera. Chabwino...Ndi kusinthana pakati pa awiriwa, nkulondola uko?) [*Awa* ndi amene ali abwino ndipo *awo* si abwino.”] (Chabwino. Zikomo inu M'bale Gene. Chabwino.)

¹⁸ Tsopano ife tiyesetsa kuti titulukenso molawirira usikuuno, kuti tidzathe kubwerera mawa usiku ndi kudzatenga mibadwo iyi. Ndipo ine ndikukuuzani inu, ndi kovuta kwambiri kuti ine ndigwire zina mwa zinthu zazikuluzo zimene ziri pansu mmphepete mwa msewu; kungoyesera kuti ndizitulutse izo zonse mu usiku umodzi. Inu mukudziwa, ndiwo mtundu wa chikhalidwe changa, koma ife tizingozigwira izo pang'ono kufikira usiku uliwonse.

¹⁹ Tsopano, basi ife tisanayambe kutsegula Bukhu lopambanali, ndikudabwa ngati ife tingakhoze kuyima kwa mphindi yokha kwa...Sinthani malo anu a...pamene ife tikuimirira, iwo amene angathe. Ndipo tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, mwaulemu, kwa mawu a pemphero:

²⁰ Atate wathu Akumwamba, ife tikubweranso kuyandikira Mpando Wanu wopambana Wachifumu Woyera, tikubwera popanda kugwedeza kwa chikhulupiriro, chifukwa ife tikubwera chifukwa ife tafunsidwa kuti tibwere. Ife sitinganene kuti ife tikubwera mu dzina la mpingo wina kapena chipembedzo, kapena mu dzina la mpingo uno, kapena mu dzina lathu lomwe, chifukwa ife sitingakhale otsimikiza za zimenezo, kuti kodi ife tingapeze kuyankhulidwa uku ndi Mulungu kapena ayi. Koma pamene Yesu anatiuza ife, “Inu mukapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho,” ndiye ife tikudziwa kuti ife tikubwera mu Dzina la Yesu, Inu mutimwa ife, Atate.

²¹ Ndife okondwa kwambiri pamene ife tiwerenga za ofera a masiku amene anapita, momwe iwo ankasindikizira umboni wawo ndi magazi awo omwe, ndiye, Atate, izo zimatipangitsa ife kumverera kuti ife tikuchita zochepa mu tsiku lino. Ndipo ine ndikukupemphani Inu, Ambuye, kuti Inu mukhululukire kwathu—kwathu—kunyalanyaza kwathu, monga ife tiriri, pa ntchito Yanu. Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutidzoze ife mwatsopano pamene ife tikuwerenga Mawu Anu, ndi kuwona kuzunzika kumene kunkabweretsedwa mmasiku apitawo kuti zikapange nsonga ya Mpingo wawukulu wowomboledwa uwu wa Mulungu wamoyo.

²² Ine ndikukupemphani Inu, Atate Akumwamba, kuti muyankhule usikuuno kudzera mwa ife chifukwa ife sitimadziwa choti tiyankhule; ife tikungoyembekezera ndipo ife tikupempha pemphero ili apa chifukwa ife tiri mu Kukhalapo kwa Mulungu mu Mpingo Wake, ndipo ife tikupemphera kuti Mzimu Woyera umene uli pa anthu awa ulumikizitse mphamvu Zake palimodzi usikuuno ndipo ukagwedeze Uthenga mu mtima uliwonse, zomwe zitipatse ife mayimidwe atsopano ndi chiyembekezo chatsopano cha m’badwo umene ukubwera. Perekani izi, Ambuye, pakuti ife tikuwona mtengo wa mkuyu ukuphukira masamba ake ndipo Israeli akukhala fuko, ndipo masiku a Amitundu akuzimirira ndipo akuwerengeka, ndipo ife tikuyembekezera kudza kwa Muomboli wamkulu, Ambuye wathu Yesu Khristu.

²³ Muyende pakati pathu, Ambuye. Monga zanenedwa usikuuno, “Inu mukuyenda pakati pa zoyikapo nyali,” ndiye muyende pakati pathu usikuuno, Ambuye. Ndipo muchenjeze mitima yathu za zoipa zomwe ziri patsogolo pathu, ndipo mutipatse ife kumvetsetsa kwa Mawu Anu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen. Mukhoza kukhala pansu.

²⁴ Tsopano, monga ine ndikumanena tsiku lirilonse, ine ndikuyesetsa kuti ndizilemba zochuluka kwambiri pa pepala monga momwe ine ndingathere, za nthawi, malo, ndi zina zotero, chifukwa ndi chochitika cha mbiriyakale chimene ife tikuchiyandikira. Iyo yakhala ili mbiriyakale, ndipo tsopano ife tikubwera kuno, nafenso, kudzazifanizitsa izo ndi nthawiyi.

²⁵ Tsopano, Lamlungu mmawa ndi Lamlungu masana... kapena Lamlungu usiku, kani, ife tinali ndi nthawi yaulemelero. Ine ndikutsimikiza ife tinatero. Ine ndinatero, inemwini. Ndi za Vumbulutso...

²⁶ Tsopano, kodi ife tikuphunzira chiyani? Vumbulutso la Yesu Khristu. Ndipo kodi ife tinapeza kuti Mulungu anawonetsa kuti vumbulutso ndi chiyani ndi yemwe Iye anali? Chinthu choyamba chimene ife tikuchipeza, mwa mavumbulutso onsewa, nchakuti Mulungu akutidziwitsa yemwe Iye anali. Kutu, Yesu sanali munthu wachitatu wa utatu, Iye anali utatu mokwanira. Iye

anali zonse Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Ndipo limenelo linali vumbulutso. Anayankhula kanayi mmutu womwewo, kuti Iye ndi Mulungu Wamphamvuzonse; Iye amene anali, amene ali, ndipo adzabwera; Muzu ndi Mphukira ya Davide.

²⁷ Tsopano ife tikupeza kuti, ndiye, kuti mu zinthu izi ife tidzayesa kudzafotokoza nkhani yonseyo, chifukwa ine sindikudziwa kuti tidzazimvanso kenanso liti Zimenezi, mwina sitidzateronso, kufikira kuti nthawi siidzakhala ponso ndipo idzaziralira mu Muyaya. Ndipo tsopano, monga ine ndimanenera, pakhoza kukhala abale ambiri, aphunzitsi oyenera bwino kwambiri kuti ayankhule izi kuposa momwe ine ndingachitire, ndipo mwinamwake akhoza kupeza kutanthauzira kwabwino kwa izo, koma Mulungu waziyika izo pa mtima wanga kuti ndichite izi ndipo chotero ine ndingakhale wachinyengo ngati ine sindinganene basi ndendende zimene ine ndikuganiza kuti ndi zolondola. Mukuona? Chotero, ine—ine nthawi zonse ndimafuna ndizimvetsedwa pamaso pa Mulungu, pa nthawi zonse, kuti “Ine sindinaleke,” monga Paulo ananenera, “kukuchenjezani inu usana ndi usiku, ndi misonzi, kuti mpingo ukhale utayima pamenepo.” Ngati pati padzakhale wotayika aliyense, magaziwo asadzakhale mmanja mwanga, chifukwa ine ndikufuna kuti ndidzakhale wopanda magazi a anthu onse panthawi imeneyo. Chotero ngati inu mukutsutsa, bwanji, ndizo, basi mwanjira yabwino yaubwenzi, izo zingakhale zabwino basi. Tsopano, koma, mwinamwake Ambuye awulula chinachake chomwe chingatithandize ife tonse, pamodzi.

²⁸ Tsopano, chinthu choyamba, ife tikuwona kuti Iye anadziulula Yekha. Tsopano ife tikumvetsa yemwe Iye anali.

²⁹ Tsopano, kumatsika mmusi, monga ine ndimapangira chobwereza chimenecho chokhudza kukonkha, ndi ubatizo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” kukhala ubatizo wa Chikatolika ndipo osati wa Chiprotestanti kapena wa Chipangano Chatsopano, ine ndikuyembekeza kuti ndazipanga izo momveka. Ndipo ine ndamufunsa munthu aliyense yemwe angandisonyeze gawo la Lemba pomwe aliyense anabatizidwapo mu Baibulo kapena kufikira ku Laodicean Council komwe iwo anakahazikitsa mpingo wa Katolika, pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” chonde abwere adzandiwonetse ine. Ndipo ine ndidzalembe ku nsana kwanga, “mneneri wabodza,” ndi kupita kumakayenda mu msewu. Tsopano, ine ndikungopanga zimenezo...osati kuti ndikhale wokaka, koma kungoti ndikuwonetseni inu kuti ndi Choonadi. Mukuona?

³⁰ Tsopano, ndiye Baibulo likumuwulula Iye apa, kuti Iye ndi Mulungu Wamphamvuzonse, mthupi pakati pathu. Mukuona? Palibe Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera; si amulungu atatu, kapena Mulungu mmodzi atadulidwa mmalo atatu. Ndi

Mulungu mmodzi yemwe amagwira ntchito mmaudindo atatu: Utate, Umwana, ndi Mzimu Woyera. Mulungu anadzitsitsa kuchokera kumunda wa Edeni, kuyesetsa kuti adzapange njira Yake yobwererera mmitima ya anthu, kuti adzakhale moyo ndi kudzakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu kachiwiri ndi Iye. Zimenezo ndi Mulungu pamwamba pathu, Mulungu nafe, Mulungu mwa ife. Ndiko kusiyana kwake. Mukuona?

³¹ Ndipo tsopano zinthu zimenezo, ndipo Baibulo limaulula zimenezo ndipo lanena zimenezo mwabwinobwino mu mutu wa 1 wa Chivumbulutso; limene liri Bukhu lokhalo mu Baibulo, mu Chipangano Chatsopano, nsonga yonse ya Chipangano Chatsopano, ndi Bukhu lokhalo limene Yesu anaikapo chisindikizo Chake pa ilo. Ndipo Iye anati, kumayambiriro kwa Ilo, “Wodala ndi iye amene awerenga ndi iye amene amvetsera.” Ndipo kumapeto, Iye anati, “Ngati munthu aliyense adzachotsera gawo lirilonse la Ilo, kapena kuwonjezera chirichonse kwa Ilo, zomwezo zidzachotseredwa, gawo lake, kuchoka mu Bukhu la Moyo.” Chotero ndi themberero kuti aliyense achotse chirichonse, ili ndi Vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu. Chotero ngati ife timupanga Iye atatu, inu mukudziwa zomwe zachitika. Mwaona, dzina lanu latulukamo.

³² Ndipo palibe aliyense, palibe wa Chiprotestanti, palibe mpingo woyambirira womwe unkakhulupirira konse mwa milungu itatu. Iyo inali nkhani yayikulu ku Nicene Council, ndipo awiri onse a iwo anapita pa nthambi; anatulukira mbali *iyi*, mwa kuyankhula. A *utatu*, anthu a patatu omwe amakhulupirira mu utatu, omwe pamapeto pake anadzapangidwa nkumakhala mu mpingo wa Katolika, iwo anapita kukakwaniritsa utatu, kumupanga Mulungu kukhala anthu “atatu”. Ndipo panali mmodzi amene anakhulupirira kuti Mulungu anali “mmodzi,” ndipo iwo anapita mbali yinayo kukakhala *aumodzi*. Awiri onsewo akulakwitsa. Mulungu sangatero . . .

³³ Yesu sangakhale atate Ake omwe, ndipo Yesu sangakhalenso ndi atate ndipo Iye nkukhala . . . pangakhale amulungu atatu. Izo—izo sizingagwire ntchito. Chifukwa ngati Iye ali ndi atate, ndipo atate nkukhala munthu wina osati Iyeyo, ndiye Iye anali . . . ndipo Mzimu Woyera ndi wina, Iye ndi mwana wapathengo. Baibulo linanena kuti Mzimu Woyera unali Atate Ake. Ndipo ngati ife tiri ndi Mzimu Woyera, ndiye kuti si Mzimu Woyera, ndi Atate mwa ife mu dzina la Mzimu Woyera, ukugwiritsa ntchito udindo mwa ife, chifukwa nthawi ina unali mwa munthu wotchedwa Mzimu, ndipo wabwereranso ndipo Iwo uli mwa ife tsopano, Yehova Mulungu yemweyo. Mukuona?

³⁴ Palibepo amulungu atatu. Amulungu atatu ndi chikunja ndi kusakhulupirira, ndipo izo zinachita kubweretsedwa. Ndipo ngati inu mutakhale sabata yonseyi ndipo osakhala atsankho, koma kupenyererera, kuzitenga izo, mbiriyakale. Kutenga

mberizakale zomwezo zomwe ine ndimazitenga kapena aliyense, mbiriyakale iliyonse. Imangokudziwitsani izo, kuti mberizakale zonse zimagwirizana chimodzimodzi. Azambiriyakale amenewo alibe chochita ndi mbali iliyonse, iwo amangokhala ndi chidwi chofotokoza mfundo, zomwe zinachitika. Ndipo penyani ndendende momwe chinthu chimenecho chinadzalowerera kudzera mwa Luther ndi kudzatuluka kudzera mwa Wesley, kenako nkudzawululidwa mmasiku otsiriza, ubatizo mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ingopenyani pamene izo zinadzalowera mu mpingo wa Katolika, mu Mibadwo Yamdima, zinadzatulukira kudzera mwa Luther, kutsika kudutsa Wesley, koma pakati pa Wesley ndi Laodikaya (kumapeto) izo zinali zoti zidzayalutsidwa. Uko nkulondola. Tsopano, ndipo yonseyi ndi mbiriyakale, ndipo osati mbiriyakale yokha, koma ilo ndi Baibulo.

³⁵ Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikufika ku Mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mpingo imene inali mipingo isanu ndi iwiri yomwe inali ku Asia Minor panthawi yomwe ankalemba Bukhuli. Mipingo iyi pa nthawi imeneyo iyenera kuti inali ndi makhalidwe a mibadwo ya mpingo yomwe inali ikudza, chifukwa chakuti . . . Kunali mipingo yambiri kuposa imeneyo, mpingo wa ku Kolose ndi ina yambiri panthawi imeneyo, koma Mulungu anasankha mipingo iyi chifukwa cha makhalidwe awo.

³⁶ Tsopano, ife tikupeza kuti Iye ataima pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide, Iye anali nazo mdzanja Lake nyenyezi zisanu ndi ziwiri. Ndipo nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimenezo, Iye anati, mu ndime ya 20 ya mutu wa 1, kuti “Iwo ndi angelo asanu ndi awiri ku mipingo isanu ndi iwiri.”

³⁷ Tsopano, mu Baibulo iwo sankalimvetisa Vumbulutso ili. Chifukwa, izo zikanawachitira iwo ubwino wanji kumayang'anira ndi kudikirira ngati iwo akanamadziwa kuti padzakhala zaka masauzande ambiri Yesu asanabwere? Izo sizinaperekedwe kwa iwo.

³⁸ Ndipo ine ndikunena kwa ichi, kwa anthu inu pano, inu anthu Achikatolika, kwa inu Achilutera, kwa inu Amethodisti, ndi ena otero, izo sizinaperekedwe kwa Martin Luther, Kuwala komwe kuli pa Mawu lero. Komanso iko sikunaperekedwe kwa John Wesley. John Wesley analalikira kuyeretsedwa kumene Luther anakulambalala. Ndipo Kuwala kumadza pamene ife tikukusowa Kuwalako. Mulungu wazinena Izo, ndipo Izo sizinatsegulidwe kwa ife chifukwa Izo zabisika mmaso mwathu mpaka tsiku limene Mulungu adzakhoze kuziwulula Izo. Ndikudabwa kuti chidzakhala chiyani ife tikadzachoka? Eya, ndine wokakamizidwa kuti pali zambiri, zambiri zomwe ife sitikudziwa kanthu za izo. Uko nkulondola. Pali Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, ngati ife titangotenga Bukhu lathunthu la Chivumbulutso, zimene zinasindikizidwa kuchikutiro cha Bukhu. Sizinati nkomwe . . . sizinalembedwe mu Bukhu. Ndipo

Zisindikizo zimenezo ndi zoti zidzatsegulidwa mu m'badwo wa mpingo uno, ndipo zinsinsi zisanu ndi ziwiri zotsiriza za Mulungu ziyenera kuti zidz- . . . zidzadziwike. Oh, ine ndikufuna kuti ndidzangokhala nazo izo mu nthawi ya chisanu yonseyo ndi kudzadutsamo Mmenemo. Inde, bwana! Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo.

³⁹ Monga Daniele anamva mabingu asanu ndi awiri, ndipo analetsedwa; ndipo Yohane anamva maliwu, ndipo Bukhu ili linasindikizidwa, ndipo kuchikutiro kwa bukhu kunasindikizidwa ndi Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri; koma mmasiku a Zisindikizo izi kuti zitsegulidwe, “Chinsinsi cha Mulungu chidzatsirizidwa.” Mwa kulankhula kwina, Mulungu adzadziwika kwa Mpingo Wake; osati mwa anthu atatu, koma ngati Munthu mmodzi. “Chinsinsi cha Mulungu chikanadzawululidwa,” ndipo pamene zimenezo zidzawululidwa kwathunthu, ndiye zinsinsi seveni zidzatsegulidwa kwa Mpingo; chifukwa, mmenemo, Mpingo uzidzakhala pansu pa kudzoza kwa Mzimu Woyera, Iye akulowamo ndi kumatuluka ndi kumawonetsera zizindikiro Zake zokhala wamoyo ndikuti ali pakati pathu, akukhala moyo pakati pathu, ndipo zikamadzatero ndiye kuti tikupembedza Khristu wamoyo yemwe ali pakati pathu.

⁴⁰ Musati muziyang'anira konse matchalitchi akuluakulu ndi zinthu zikuluzikulu. Pamene ife tidzafika ku m'badwo wa Pentekoste uwu, inu ndithudi mudzawona pomwe iwo anazitayira. Mpingo kumene wa *Laodikaya* umatanthauza “olemera, osasowa kanthu,” ndi wamaliseche, watsoka, wakhungu, womvetisa chisoni, ndipo sakudziwa izo ayi. Mukuona? Iwo anasochera pofuna kutsatira ndalama zochuluka, ndi nyumba, ndi china chirichonse.

⁴¹ Pamene, Mpingo nthawizonse wakhala uli zo—zopanda ntchito za padziko lapansi. Ndipo apa iwo anali: akudedwa ndi anthu onse, amathamangitsidwira panja, mmakwalala, kulikonse kumene iwo angakakhaleko. Werengani Ahebr 11, ndipo mutenge ndime zomalizira sikisi kapena eyiti za iwo, momwe “iwo amayendayenda mu zipululu, ndipo—ndipo amavala zikopa za nkhosa ndi zikopa za mbuzi, ndipo anali osowa pokhala, ndipo amasautsika, ndi kuzunzidwa.” Anthu amenewo kumeneko, kodi umboni wathu udzaima bwanji motsutsana ndi wawo pa tsiku la Chiweruzo? Mwawona, anthu amenewo mu tsiku limenelo.

⁴² Tsopano, mu m'badwo wa mpingo uwu. . .Ife tiri ndi mipingo isanu ndi iwiri, tsopano ine ndikufuna ndizikhazikitse izo. Ine sindikuganiza kuti inu mukutha kuziwona izo kuchokera apa, mwinamwake ngati ena a inu mungathe, ine ndikukaika izo kwambiri, koma ine ndiyesetsa kuti ndizipange izo, (ine ndikudziwa inu simukanakhoza, mutakhala pansu muno),

kupangitsa kuti imveke Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Ine ndizigwira izo mdzanja langa kuti inu mumvetsetse.

⁴³ Iwo ukuyambira, Mpingo unayambira pa Pentekoste. Kodi wina angakhoze kukana zimenezo? Ayi, bwana! Mpingo unayambira pa Pentekoste ndi Mdalitso wa Pentekoste, ndipo unadzozedwa ndi Yesu Khristu kuti ukapitirire mpaka tsiku lomaliza ndi Uthenga womwewo ndi mdalitso womwewo ukugwira ntchito mwa ife. Kutuma Kwake kotsiriza ku Mpingo Wake, Marko 16, “Pitani ku dziko lonse, kalalikireni Uthenga, zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Tsopano, kutiko? “Ku dziko lonse lapansi.” Kwa ndani? “Cholengedwa chirichonse.” Wakuda, wabulauni, wachikaso, woyera, cholengedwa chirichonse chomwe chinali, kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Tsopano, usikuuno ife tiri pa mpeni wa zimenezo, zikungoyamba kudula pakati usikuuno, usiku uliwonse zizidula chidutswa chokulirapo cha Izo mpaka ife titafika ku m’badwo wa mpingo wathu womwe. Tsopano, ife tikupeza kuti uko kunali kutuma Kwake.

⁴⁴ Tsopano, m’badwo wa mpingo woyamba unali mpingo wa ku Efeso. M’badwo wa mpingo wachiwiri unali Smurna. M’badwo wa mpingo wachitatu unali Pergamo. M’badwo wa mpingo wachinai unali Tiyatira. M’badwo wa mpingo wachisanu unali Sarde. Ndipo m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chimodzi unali Filadelfiya. Ndipo m’badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri unali Laodikaya.

⁴⁵ Tsopano, m’badwo wa mpingo woyamba unayamba cha mu A.D. 53, pamene Paulo anakhazikitsa mpingo ku—ku Efeso. Paulendo wake waumishonare, iye anakhazikitsa mpingo ku—ku Efeso, mpingo wa ku Efeso, ndipo anali m’busa wa iwo kufikira pamene iye anadzadulidwa mutu mu 66, kumupanga iye pafupifupi zaka twente thuu kukhala m’busa wa mpingo wa Efeso. Itachitika imfa yake ndiye ife timauzidwa kuti Paulo Woyera . . . kapena Yohane Woyera waumulungu anakhala m’busa wa mpingo ndipo anawupitiriza iwo mpaka ku m’badwo uno, ndipo m’badwo wa mpingowo unapitirira mpaka 170.

⁴⁶ Ndiye utatha M’badwo wa Mpingo wa Efeso, kuyambira A.D. 53 mpaka A.D. 170, ndiye panayambika M’badwo wa Mpingo wa Smurna womwe unakhala mu A.D. 170 mpaka A.D. 312. Kenako kunadzabwera M’badwo wa Mpingo wa Pergamo, ndipo M’badwo wa Mpingo wa Pergamo unayamba 312 ndipo unadzakhala mpaka A.D. 606. Zitatero kunadzabwera M’badwo wa Mpingo wa Tiyatira, ndipo m’badwo wa mpingo wa Tiyatira unayamba pa 606 ndipo unapita mpaka ku 1520, Mibadwo ya Mdimu. Ndiyeno M’badwo wa Mpingo wa Sarde unayamba mu 1520 ndipo unapitirira mpaka 1750, m’badwo wa Lutera. Ndiye kuyambira 1750, m’badwo wotsatira umene unadzabweramo unali wa Filadelfiya, m’badwo wa Wesley; umene unayamba mu

1750 ndipo unadzafika mpaka 1906. Ndipo mu 1906 M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya unayambika, ndipo ine sindikudziwa kuti iwo udzatha liti, koma ine ndikuneneratu kuti iwo udzatha pofika 1977. Ine ndikuneneratu, osati Ambuye andiuzwa ine, koma ine ndikuneneratu izo molingana ndi masomphenya omwe ndinawonetsedwa zaka zingapo zapitazo, kuti, faivi mwa zinthu zimenezo zachitika (mwa seveni) zinachitika kale.

⁴⁷ Pafupifupi... Ndi angati akukumbukira masomphenya amenewo, mu tchalitchi? Ndithudi. Ndinanena zimenezo, momwe ngakhale Kennedy adzasankhidwire mu zisankho zapitazi. Momwe akazi adzalolezedwere kuvota. Momwe Roosevelt angadzalitengere dziko kupita ku nkondo. Momwe Mussolini akanadzapita molunjika ku Ethiopia, kuwukiridwa kwake koyamba, ndipo akanadzatenga ilo; amenewo adzakhala mapeto ake, iye akanadzafa zikadzachitika zimenezo. Momwe ma ism aakulu awa ati adzawukire ndipo onse nkudzagwa kubwerera mu Chikominisi; Hitlerism, ndi Mussolini, ndi Co-... Nazism, ndi zina zotero, zonse zikanadzagwa kubwerera ku Chikominisi. Ndipo zaka leveni zisanachitike, izo zinati "Ife tikanadzapita ku nkondo ndi Germany, ndipo Germany adzakhala wotetezeka kuseri kwa konkire," Mzere wa Maginot. Izo zinadzachitika mwanjira imeneyo basi. Ananena pamenepo, zitachitika zimenezo, zikanadzafika pamalo akuti... zidzachitika kuti sayansi idzakwera kwambiri mpaka iwo akanadzapanga galimoto, magalimoto akanadzakhala ofanana ngati "dzira" nthawi zonse. Ndipo masomphenya amenewo anadzanenedwa pomwe pano pamene Mpingo wa Khristu wamangidwa pano, ku Mes-... kunyumba ya ana amasiye. Charlie Kern, mwinamwake mu chipinda usikuuno, ankakhala kumeneko panthawiyo. Lamlungu lina mmawa pafupifupi 7 koloko izo zinadzachitika. Ndipo Iwo anati, "Kenako pamenepo zidzachitika kuti iwo adzapanga galimoto yomwe siimadzasowekera chiwongolero mmenemo, iyo izidzayendetsedwa ndi mtundu wina wa mphamvu." Iwo ali nayo iyo tsopano. Iwo ali nayo iyo tsopano, mu mphamvu yamaginito, yowongoleredwa ndi makina amlengalenga. Iwo samayesera nkomwe... umangokhazikitsa makina ako mmwamba kumene iwe ukupita, izo zimatengera iwe mwini, iwe sumasowa kuti uzichita kuwongolera.

⁴⁸ Tsopano, ndipo iwo ananena pamenepo, "Pa nthawi imeneyo, padzakhala mkazi wamkulu adzaimirire mu United States." Ndipo iye anali atavala ndipo akukongola, koma anali mthakati mu mtima. Ndipo ine ndinaziika m'mikutiro mu zolemba pa masomphenya, ngakhale pepala lachikaso, ndinati, "mwinamwake mpingo wa Katolika." Ndipo akazi kulolezedwa kuvota zidzathandizira kusankha munthu wolakwika kwa fuko lino. Ndipo ndizo zomwe iwo anachita. Ndendende. Tsopano, anati, "Ichi chidzakhala chiyambi."

49 Tsopano chinthu china chimene iwo ananena, kuti... Ndiye nthawi yomweyo zitachitika zimenezo, Ine ndinawona fuko lino likukhala ngati likufuka, likungophulika mzidutswa. Tsopano, ngati zinthu zimenezo zachitika, chomwechonso china ichi. Ife tiri pa... Ndi chifukwa chake ine ndiri pano usikuuno kuyesetsa kuti ndibweretse izi ndi kuziyika izo kwa anthu awa ku Jeffersonville, chifukwa ndikukonzekera kuti ndikalowe mminda yaumishonare posachedwapa kenanso, ndipo sindikudziwa kuti ndi nthawi yanji nditi ndidzaitanidwe kapena kudzatengedwera kutali. Ine—ine... ife sitikudziwa zimenezo. Ndipo ine ndikufuna kukhala wotsimikiza kuti ndiri... kuwulola mpingo kuti udziwe ora limene iwo ukukhalamo, chifukwa Mulungu Wamphamvuzonse adzandiyimba ine mlandu chifukwa cha zimenezo.

50 Tsopano—tsopano, uliwonse wa mipingo iyi, molingana ndi Lemba pamenepo, unali ndi mngelo. Ndipo mngelo anali... Ndi angati amadziwa chimene *mngelo* amatanthauza? Ndi “mthenga,” mthenga. Ndipo pamenepo—pamenepo panali *angelo seveni* ku mipingo seveni, kutanthauza “atumiki seveni.” Tsopano, ndipo iwo anali nyenyezi mdzanja Lake. Ndipo mdzanja Lake awa—thwelofu awa... nyenyezi seveni izi zomwe zinali zoti zikanyezimiritse Kuwala kwa Kukhalapo Kwake mu tsiku la usiku limene ife timakhalamo. Monga nyenyezi zimanyezimiritsa dzuwa padziko lapansi, zimapangitsa ilo kuti liwale kuti ife tikhoze kumayendamo, komanso kuyenda mozungulira nthawi yausiku.

51 Tsopano ife tikupeza ndiye, kuti panthawi iyi, kuti mmodzi aliyense wa angelo amenewo anali ndi udindo ndi malo. Ndipo, abale, usikuuno ife sitifika kwa izo, chifukwa ife tikumudziwa mngelo uyu wa mpingo woyamba, koma icho chikhala chinthu chachinsinsi ndi chaulemelo kuchipeza ndi kuchitulutsa kuchokera mu mbiriyakale, pamaso panu, angelo a mipingo ina iyi. Mngelo wa mpingo woyamba anali Paulo Woyera, iye anauyambitsa iwo, mthenga wa Mulungu. Mngelo wa mpingo wa ku Efeso anali Paulo Woyera. Mpingo... Tsopano, chifukwa chimene ine...

52 Tsopano, ena awa inu mwina mukhoza kusagwirizana nazo, koma ine ndakhala pamenepo kwa masiku ndi masiku pansu pa kudzoza mpaka ine ndinamverera Mzimu Woyera ukundikhudza ine ndi kundidzoza ine chifukwa cha zimenezo. Ndi chifukwa chake ine ndikudziwa. Ndipo muwone amuna awa omwe asankhidwa, ngati ndinu wa zambiriyakale, iwo... Amuna omwewo omwe ndiri nawo pano, ndipo ndikudziwa mwa vumbulutso kuti iwo anali angelo ku mpingo, iwo anali ndi utumiki wofanana ndi umene iwo anali nawo pachiyambi. Ndipo utumiki umenewo sungasinthe, iwo ukuyenera kukhala pentekoste kudutsa njira yonse.

⁵³ Tsopano, azambiriyakale amene akhala apa atsutsana nane za munthu uyu; koma pa mpingo wa Smurna, Ireniasi ndi yemwe ine ndikudziwa kuti anali mngelo wa tsiku limenelo. Polycarp, ambiri a inu munganene kuti anali Polycarp, kani, inu munganene kuti anali iyeyo. Koma Polycarp ankatsamira kwambiri ku bungwe ndi kwa Katolika, chipembedzo chimene chimabwera. Koma Ireniasi anali munthu yemwe ankayankhula mmalirime, ndipo anali nayo mphamvu ya Mulungu, ndipo zizindikiro zinkamutsatira iye. Iye anali Kuwala kwa mngelo wa Mulungu, ndipo iye anakokera Kuwala nkumapitirira nako Polycarp atapachikidwa kapena ataphedwa, atanyongedwa, ndiye Ireniasi anali mmodzi wa ophunzira ake, ndipo Polycarp anali wophunzira wa Paulo Woyera. . . kapena Yohane Woyera. Ndiyeno Ireniasi anadzatenga malo ake, ndipo anadzabweretsa Kuwala.

⁵⁴ Ndipo mngelo wa Kuwala kwa—kwa Pergamo anali Martin Woyera wamkulu. Ine sindikukhulupirira kuti panakhalapo munthu wamkulu padziko lapansi, kunja kwa Yesu Khristu, kuposa Martin Woyera. Mphamvu? Opha anthu anabwera kwa iye kuti adzamudule mutu (iye ankakhulupirira mu zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi Mdalitso wa Pentekoste), ndipo pamene iwo amapita, iwo amapita kuti akamuphe iye, iye anakokera chovala chake ku nsana ndipo anakwezera khosi lake kwa iwo. Ndipo pamene wakuphayo anasolola lupanga kuti adule mutu wake, mphamvu ya Mulungu inamugwetsera iye kutali ndi iye, ndipo iye anakwawa ndi maondo ake kuti akamupempe iye. . . ? . . . Ameni. Iye anali mngelo ku mpingo.

⁵⁵ Zinthu zina. Penyani momwe iye. . . Mmodzi mwa abale ake anali atapachikidwa, iye anali panjira kuti akamupeze iye, onani zimene zinachitika. Ndipo pamene iye anakafika kumeneko, iwo anali atamupachika kale iye. Iye anali atagona, atafa, ndipo maso ake anatuluka mmutu mwake. Iye anakalowa kwa iye ndipo anakagwera pansu pa mawondo ake ndipo anakagoneka thupi lake pa iye kwa ora, akupemphera kwa Mulungu. Ndipo mphamvu ya Mulungu inabwera pa munthuyo ndipo iye anauka, anamugwira dzanja lake ndipo anachokapo ndi iye pomwepo. Imeneyo ndi mbiriyakale, chimodzimodzi monga George Washington, Abraham Lincoln, kapena enanso. Ndi mbiriyakale.

⁵⁶ Inde, bwana! Martin Woyera anali mngelo wa mpingo wa Pergamo, umene, mpingo wachikwati chimene chinawatengera iwo kupita mu Chikatolika zitachitika zimenezo.

⁵⁷ Mngelo wa mpingo wa—wa Tiyatira anali Columba.

⁵⁸ Mngelo wa mpingo wa Sarde, mpingo wakufa. . . Mawu akuti *Sarde* amatanthauza “wakufa.” Anatulukako ndi dzina, osati Dzina Lake, “Koma dzina lakuti uli moyo, koma ndiwe wakufa.” Penyani momwe iwo anawubweretsera ubatizo umenewo mu tsiku limenelo. Mwawona, chokaniko kwa izo.

Mngelo wa mpingo wa Sarde anali Martin Luther, wokonzanso woyamba.

⁵⁹ Mngelo wa mpingo waku Filadefiya anali John Wesley, mthenga.

⁶⁰ Ndipo mngelo wa mpingo wa—wa Laodikaya sakudziwika panobe. Izo zidzakhala tsiku lina, koma mwinamwake iye . . . ali padziko lapansi, “Iye amene ali nalo khutu . . .” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . mudziwe kuti uwu ndi m’badwo umene ife tikukhalamo. Mulungu adzachita kuweruza kwa izo.

⁶¹ Tsopano, zindikirani tsopano, ndipo ife tifika tsopano ku Malemba, kubwerera ku m’badwo wa mpingo woyamba. Tsopano ine ndikufuna . . . Ine ndiri ndi zinthu zina pang’ono ndazilemba apa zomwe ine ndikukhumba inu mukanati muzimvetsera mwatcheru.

⁶² Mpingo woyamba, mpingo waku Efeso, ntchito za mpingo, chimene Mulungu ankawatsutsira iwo, chinali ntchito zopanda chikondi. Mphotho yawo inali Mtengo wa Moyo.

⁶³ Mpingo wa Smurna unali mpingo wozunzidwa, unadutsa mmasautso. Mphoto inali korona wa Moyo.

⁶⁴ Mpingo wachitatu, Pergamo, m’badwo wa chiphunzitso chabodza, bodza la Satana, ndi maziko a ulamuliro waupapa, chikwati cha tchalitchi ndi boma. Mphotho yake inali mana obisika ndi mwala woyera.

⁶⁵ Mpingo wa Tiyatira unali mpingo wa kudolola kwa upapa, Mibadwo ya Mdima. Mphotho inali mphamvu ndi kulamulira kwa mafuko, ndi Nyenyezi ya Mmawa. Ndiwo ochepa kwambiri amene anadutsamo.

⁶⁶ Mpingo wa Sarde unali m’badwo wokonzanso, umishonare wawukulu . . . kapena osati umishonare, koma maina obisika, iwo anali nawo maina awo awo. Ndipo mphotho yake inali chovala choyera, ndi dzina pa Bukhu la Moyo (lomwe liyenera kudzabwera mu chiweruzo). Ife tinali nazo izo tsiku lina, Bukhu la Moyo; inu ndi woti mudzaweruzidwa kuchokera mu Bukhu la Moyo. Oyera adzasandulizidwa ndipo adzatengedwa popanda zimenezo, iwo sadzapita ku zimenezo.

⁶⁷ M’badwo wa Mpingo wa Filadelfia unali m’badwo wa chikondi cha pa abale, m’badwo wa kutumidwa kwakukulu ndi m’badwo wa umishonare wopambana, khomo lotseguka. Ndipo mphotho inali mza—mzati. Kuwulula maina a Mulungu kumayenera kukhala mu—mu m’badwo uwu, pamene iwo unatuluka cha mu 1906. Chabwino.

⁶⁸ M’badwo wa Laodikaya unali mpingo wofunda, wolemera, wochulukidwa ndi katundu, wosasowa kanthu; koma unali womvetsa chisoni, wosauka, wakhungu, ndi womvetsa chisoni, ndi wamaliseche. Ndipo mphotho inali ya kudzakhala pa

Mpandowachifumu ndi Ambuye, iwo amene adzagonjetse m'badwo umenewo.

⁶⁹ Tsopano kuti ndizigawegawe, usikuuno, kuti ndikusonyezeni inu pang'ono za msonkhano usikuuno, ife titenga mutu wa 2, m'badwo wa mpingo woyamba. Tsopano ife...

Iye akuwululidwa ndipo ife tikudziwa yemwe Iye ali, Iye ndi Mulungu!

⁷⁰ Tsopano, m'badwo wa mpingo unayamba monga ine ndinanenera pafupifupi 53, mpaka 170. Ndipo (a) mzinda wa Efeso, umodzi mwa mizinda itatu yayikulu ku Asia; kawirikawiri umatchedwa mzinda wachitatu wa chikhulupiriro cha Chikhristu (woyamba unali Yerusalemu; wachiwiri, Antiokeya; ndipo wachitatu, Efeso)...(c) mzinda wa chuma chambiri ndi malonda...(e) boma linali la Chiroma...(f) chinenero chake chinali Chigriki. Azambiriyakale amakhulupirira kuti Yohane, Maria, Petro, Andreyana, ndi Fillipo onse anakaikidwa kumeneko. Ndipo Efeso anakadziwika chifukwa cha kukongola kwake.

⁷¹ Chikhristu ku Efeso ndi kumene Ayuda anakakhalako, ku Efeso. Ndipo unakhazikitsidwa pafupifupi A.D. 53 kapena 55. Chikhristu chinabzalidwa kumeneko ndi Paulo Woyera. Mtsogolo, Paulo Woyera anakakhala zaka zitatu ku Efeso. Chiphunzitso cha Paulo chinabereka chikoka chachikulu kwa okhulupirira a ku Efeso. Kenako, Timoteo anali bishopu woyamba wa mpingo ku Efeso. Paulo analemba kwa mpingo ku Efeso. Mu nthawi ya Paulo iwo unali mpingo waukulu.

⁷² Efeso amatanthauza...dzina kumene lakuti *Efeso* limatanthauza “kuzisiya zizipita, kulekerera, kubwerera mmbuyo.” Oyitanidwa ndi Mulungu, “Mpingo wobwerera mmbuyo.” Mulungu—Mulungu anzindikira poyamba ntchito zawo, ntchito zawo, ndi chipiriro chawo. Mulungu anawadzudzula makhalidwe awo, kusiya chikondi chawo choyamba, chifukwa chobwerera mmbuyo, ndi kusakhalanso ndi Kuwala. Efeso sunali mpingo wonyengedwa, iwo unalephera wokha posapitirira mchikondi changwirowo.

⁷³ Chidule cha Efeso: Zipatso, zopanda chikondi, zinatsogolera ku chinyengo. Malonjezo: Paradiso wolonjezedwera ogonjetsa, a oyera aku Efeso mu m'badwo wa mpingo, operekedwa ku Mtengo wa Moyo.

⁷⁴ Apa pali chinthu chokongola. Mtengo wa Moyo ukutchulidwa katatu mu Genesis, katatu mu Chivumbulutso. Nthawi yoyamba yomwe unatchulidwa mu—mu Genesis, munali mu Edeni, ndipo Khristu anali Mtengowo. Nthawi zitatu zomwe unatchulidwa mu Chivumbulutso, anali Khristu mu Paradiso. Oh, ndi zakuya zimenezo. Ambuye adalitse.

75 Tsopano tikuyambira mutu wa 1 wa Aefeso. . . kapena ndime ya 1 ya mutu wa 2, mpingo wa ku Efeso:

Kwa mngelo wa mpingo wa ku Efeso lemba; Zinthu izi anena iye amene wagwira nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja lake lamanja, amene akuyenda pakati pa zoyikapo nyali seveni zagolide;

76 Yohane ndi mtu—mtumiki pa nthawi imeneyo. Akuyenda pakati pa zoyikapo nyali seveni izi anali Yesu Khristu, Mulungu Wamphamvuzonse. Kodi Iye akuchita chiyani? Iye sananene kuti Iye akuyenda mu choyikapo nyali *chimodzi*, Iye amayenda pakati pa izo zonse. Kodi zimenezo zikutanthauza chiyani? Kuti Iye ali Mulungu yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo mu m'badwo wa mpingo uliwonse kwa wokhulupirira aliyense. Iye akubwera kwa. . . ndi Mzimu Woyera ku m'badwo uliwonse ndi kwa munthu aliyense; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

77 “Atagwirizira mdzanja Lake lamanja.” *Dzanja lamanja* limatanthauza Zake “ulamuliro ndi mphamvu.” Atagwirizira mdzanja Lake lamanja (pansi, akulamuliridwa) atumiki asanu ndi awiri ku mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. Tikumuwona Iye akuyenda yenda kudutsa mibadwo ya mpingo iyi, Khristu, akudzizindikiritsa Yekha kwa anthu Ake kudutsa Mibadwo ya Mdima iyi, kutsika kumadutsa m'badwo uliwonse; pamene mpingo unadzakhala wofunda ndipo nkumachokapo, ndipo ena amapita njira ina ndi ena inayo, koma ochepa apang'ono awo a mpingo anagwiritsitsabe, ndipo Khristu ankagwira nawo ntchito, kumatsimikizira Mawu Ake; kumawazungulitsa Iwo kudutsa mmenemo.

78 Ndi zophweka kwambiri kuwona momwe tapezera zimene ife tiri nazo lero, pamene inu mwayamba kuphunzira izi. Tsopano, apa pachiyambi. . . ine ndikukhulupirira inu nonse mukukhoza kuwona pamwamba apa. [M'bale Branham akusonyezera pa bolodi—Mkonzi]. Apa pali m'badwo umodzi wa mpingo, ndiwo Pentekoste. M'badwo wa mpingo wachiwiri, wachitatu, wachinayi, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, m'badwo wa mpingo wachisanu ndi chiwiri. Tsopano ngati inu mungazindikire izi mwatcheru kwenikweni, Mpingo unayambira pa Pentekoste. Ndi angati akukhulupirira zimenezo? Inu mukuona zimene zinachitika pa Pentekoste? Ndiye ife tikuwuwona mpingo pamene iwo ukutsikira mmusi. Iwo ukungoyamba kuzimirira pang'ono pang'ono, patsogolo pang'ono, patsogolo pang'ono; pang'ono pokha, iwo ukupita pansu munga *choncho* pamene Mpingo woona weniweni ukutuluka.

79 Tsopano, Khristu. . . ziribe kanthu kuti Mpingo ndi waung'ono bwanji, “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi mu Dzina Langa, Ine ndidzakhala pakati

pawo.” Pamene iwo asonkhana pamodzi mu chiyani? Mu dzina la Methodisti? Dzina la Baptisti? Dzina la Pentekoste? Dzina la Yesu! Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana pamodzi, ziribe kanthu momwe angakhalire apang’ono. Ndipo iwo adzakhala apang’ono kwambiri mu masiku otsiriza mpaka, Iye anati, Iye adzayenera kuti adzabwere mwachangu ndi kudzaifupikitsa ntchitoyo kapena kupanda kutero sipadzakhala mnofu udzapulumutsidwire Mkwatulo. “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa!”

⁸⁰ Tsopano, kuzungulira koyamba, atumwi. Tsopano, ife tikuwona kuti uku ndiko kuyamba, Pentekoste. Iye akuyenda yenda, Mulungu wamkulu yemweyo, zizindikiro zazikulu zomwezo zinali zoti zizichitika kudutsa mibadwo iyi chifukwa Iye amayenda pakati pa m’badwo uliwonse. Amadalitsa chiyani? Anthu Ake amene asonkhana mu Dzina Lake.

⁸¹ Ine ndikufuna kuti muwone izi pamene ife tikudutsa mu mpingo. Mpingo *uwu* unali ndi Dzina la Yesu. Mpingo *uwu* unali ndi Dzina la Yesu. Mpingo *uwu* unali ndi Dzina la Yesu. Ndipo mpingo *uwu* unataya Ilo. Mpingo *uwu* unatuluka, m’badwo wa Chilutera, ndi “dzina lakuti uli moyo, koma ndiwe wakufa.” Ndipo zikupitirira mpaka mmusi mpaka kumapeto a m’badwo *uno*; ndipo pakati pa m’badwo *uwu* ndi m’badwo *uwu* pali chitseko chotseguka chomwe chikubwezeretsanso Dzinalo ku mpingo. Tsopano penyani ndipo muwone ngati icho chiri Choonadi, titatha kuzipeza izo apa mu Malemba. Pamenepo pakati pa—pa mibadwo.

⁸² Tsopano, mawa usiku ine ndidzayesetsa kuti ndidzakhale ndi izi pano kuti ife tonse tidzakhoze kuziwona izo. Ndipo ine ndidzatsikira kuno mwinamwake mawa masana ndi kudzajambula kwa . . . ena a—madongosolo omwe ine ndikufuna kuti ndiyankhule nanu. Ndipo ngati aliyense wa inu ali ndi mbiriyakale, mudzabwere nazo izo. Kapena mudzatenge zolembe zanu ndipo mudzapite ku laibulale kapena kwinakwake kuti mukapeze mbiriyakale, ndikukaiwerenga iyo ndikuwona ngati izi ziri zolondola.

⁸³ Tsopano ndime ya 1. Kodi Iye akuchita chiyani? Iye akuwapatsa iwo malonje.

Kwa—kwa mngelo wa mpingo wa ku Efeso . . . (kwa Yohane) lemba; Zinthu izi anena iye amene wagwira nyenyezi seveni mu dzanja lake lamanja, amene akuyenda pakati pa zoyikapo nyali seveni za golide; (ndi malonje)

⁸⁴ Tsopano ndime ya 2 ndi ndime ya 3, Iye akuwayamikira iwo:

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi zovuta zako, ndi chipiriro chako, . . . momwe kuti iwe sungapirire nawo iwo amene ali oyipa: ndipo iwe wawayesa iwo amene

akunena kuti ali atumwi, ndipo siali, ndipo iwe wawapeza iwo kuti ndi abodza:

⁸⁵ Mwawona, chinyengo chimenecho chinali chitayamba kale kulowa, mu m'badwo woyamba uwu. Chitayambika kale pamenepo; chifukwa osankhidwa ndi Mpingo woona amene ankafuna kusunga malamulo a Baibulo, ndi kusunga Mawu amene Yesu ananena mu umboni Wake, iwo anali atayamba kale kuchokamo. Chinachake chinayamba kuchitika, ndipo apo panali aphunzitsi abodza akuwuka, anthu amene anali kuphunzitsa molakwika, motsutsana ndi Lemba, kuyesera kuti abweretsemo chinachake kapena kuwonjezera chinachake.

⁸⁶ Ndi chifukwa chake Iye anapereka vumbulutso ili kwa mpingo ndipo anati, "Aliyense amene adzachotsa kapena adzawonjezerako, gawo lako lidzachotsedwa kuchoka mu Bukhu la Moyo." Ndiko, kutayika, m'bale! Basi musamawasokoneze Mawu a Mulungu! Ziribe kanthu yemwe Iwo akumupweteka kapena chomwe Iwo akupweteka, mungowanena Iwo mulimonse. Basi momwe Iwo analembedwera pamenepo, ndiyo njira yake. Ife sitikusowa chachikulu chirichonse, ife sitikusowa wansembe aliyense kapena chirichonse choti chiziwatanthauzira Iwo kwa ife, Mulungu Mzimu Woyera ndiye wotanthauzira. Iye amapereka kutanthauzira.

⁸⁷ Tsopano, ngati inu mungazindikire, atachoka kwa zoyipa ndipo nkukawapeza aneneri abodza, zitatha zimenezo iwo anatsimikiziridwa kuti ndi abodza, okhala nawo mawonekedwe achipembedzo. Mukuona momwe mpingo unayambira kuyamba kukhala wofunda nthawi imeneyo? Iwo anayamba mokhala ngati kumawatsitsira pansu anthu amene amakhala pansu pa kudzoza kwa Mzimu Woyera, anayamba kumawapangitsa anthu kuti aziwaseka iwo.

⁸⁸ Chabwino, kodi Yesu sananene kuti, "Odala muli inu pamene mukuzunzidwa chifukwa cha chirungamo"? Iye sananene kuti muyambe kukhala ofunda. Iye anati, "Kondwerani, ndipo mukhale okondwera kwambiri, popeza iwo anawazunza aneneri amene analipo pambuyo pa inu." Iye ananena zimenezo, ziri mu chiphunzitsi cha pa phiri, mu Mateyu 5, "Odala muli inu!" Bwanji, kuti anthu azikunyozeni inu chifukwa chakuti inu mukuwakonda Ambuye Yesu, ndi mdalitso kungoti iwo azinena zimenezo. Iwo ali kokha... Pamene iwo akukutukwanani inu, iwo akubweretsa madalitso a Mulungu pa inu. Izo zimawabwerera iwo, monga izo zinachitira pa Balamu nthawi ijayi. Izo—izo zimawabwerera iwo. Pamene iwo adzayesera kuti azikunyozeni inu chifukwa chokhala Mkristu, bwanji, izo zimawabwerera iwo, ndipo Mulungu amapereka mdalitso, chifukwa, "Odala muli inu pamene anthu adzakuzunzani inu chifukwa cha Dzina Langa." Chifukwa cha Dzina Lake, "Odala muli inu!"

⁸⁹ Tsopano ife tikupeza kuti iwo ankafuna kuyamba ndi kulowa mu mawonekedwe aumulungu.

⁹⁰ Tsopano, ine ndikhoza kuyimira pomwe apa ndi kunena chinachake, ndikukhulupirira ine nditero. Kodi inu munazindikira kuti chitsitsimutso chirichonse...Tsopano, abale otumikira, inu mufufuze izi. Chitsitsimutso chirichonse chimabala mapasa, chimodzimodzi monga momwe Yakobo ndi Rebeka anaberekera mapasa: Esau ndi Yakobo. Ine ndikutanthauza Isaki mmalo mwa...Isaki ndi Rebeka, mmalo mwa Yakobo. Isaki ndi Rebeka anabala mapasa. Abambo anali woyera, amayi anali woyera, koma iwo anali ndi anyamata awiri obadwa: Esau ndi Yakobo.

⁹¹ Tsopano, awiri onsewo anali achipembedzo. Koma Esau, zikafika pa nkhani yantchito ndi zochitachita, ngati wa zamalamulo wabwino, iye mwinamwake anali mnyamata wabwinoko, njira yonse, kuposa momwe Yakobo anali. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Yakobo anangokhala mnyamata wamng'ono yemwe amangokhala pafupi ndi amayi ake nthawi zonse. Koma Esau ankapita kunja ndipo amakagwira ntchito, amapita ndi kukatenga nyama kuti akawapatse abambo ake okalamba omwe anali mneneri, iye ankayesetsa kuwasamalira iwo. Koma Yakobo anali ndi chinthu chimodzi chokha mmalingaliro mwake, iye ankafuna ufulu woyamba kubadwa umenewo! Iye analibe nazo kanthu kuti adikirira nthawi yayitali bwanji kapena chirichonse chomwe iye ankayenera kuti achite, chinthu chofunikira pamoyo wake chinali ufulu woyamba kubadwa! Ndipo Esau ankanyoza zimenezo.

⁹² Tsopano kodi inu simukumuwona munthu wachirengedweyo—munthu wachirengedwe? Pamene chitsitsimutso chibwera, pamakhala magulu awiri a anthu amene amatulukira mu chitsitsimutso chirichonse. Pamakhala munthu wachirengedwe amene amapita, ndipo iye amabwera ku guwa ndikudzati, “Inde, bwana, ine ndikumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanga.” Iye amapita panja, ndipo kodi iye amakachita chiyani? Chinthu choyamba inu mukudziwa, iye amadzafika mu mpingo wina wabwino wozizira, wofunda, chifukwa iye amaganiza, “Chabwino, ngati ine nditajowina tchalitchi, ine ndidzakhala wabwino basi ngati munthu winayo. Kodi sindine wabwino basi ngati *Wakuti-ndi-wakuti?* Kodi izo zimapanga kusiñana kotani bola ngati ine ndiri wa tchalitchi ndipo ndikumapanga kuvomereza kwanga?” Bwanji, izo ndizosiyana kwathunthu. Iwe uyenera kubadwanso mwatsopano. Iwe ukuyenera kukhala ndi ufulu woyamba kubadwa.

⁹³ Ndipo Yakobo sanasamale kuti akusekedwa mochuluka bwanji. Iye ankafuna ufulu woyamba kubadwa umenewo, ndipo iye analibe nazo ntchito kuti iye awupeza bwanji iwo.

⁹⁴ Tsopano, anthu ambiri samafuna kukhala ndi ufulu woyamba kubadwa chifukwa iwo amaganiza kuti izo basi ndi zosatchuka pang'ono. Iwo samafuna kudzagwada pansu paguwa ndi kukalira pang'ono, kapena kukhala osadya chakudya pang'ono, ndi—ndi chinachake chimzake. Iwo—iwo—iwo—iwo samafuna kuchita zimenezo. Akazi ambiri... ochuluka a, inu mukudziwa, mani... atadziphoda, iwo amaganiza kuti ngati iwo alira iwo akhoza kutsukuluzapo izo, adzayenera kuti adzazipakenso izo kachiwiri. Bwanji, iwo... ndizo... Ndipo ine sindikutanthauza kunena izo mosinjirira, ine ndikuyembekeza izo sizikumveka mwanjira imeneyo, koma ndicho choonadi. Iwo basi samawufuna Iwo. Iwo samakufuna Kubadwa Kwatsopano, chifukwa Kubadwa Kwatsopano kumakhala ngati ndi nyansi. Izo ziri ngati kubadwa kwina kulikonse. Kubadwa kulikonse ndi nyansi, ine sindikusamala komwe iko kuli. Ngati kukuchitikira mu khola la nkumba kapena mu khola, kapena ngati muli mwa pinki, chipinda chokongoletsedwa cha ku chipatala, ndi nyansibe.

⁹⁵ Ndipo chomwechonso Kubadwa Kwatsopano kumakhala nyansi! Amen. Iko kumakupangitsa iwe kuchita zinthu zimene iwe sumaganizira kuti ungazichite; kuima pangodya ndi kumamenya nkhotcho, kapena kuimba, "Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya! Mulungu Alemekezeka! Ulemelero kwa Mulungu!" Bwanji, iwe umachita ngati wamisala. Ndi zomwe zinachitika kwa atumwi, ndi zomwe zinachitika kwa namwali Maria, iye anachita ngati waledzera. Iye anali nyansi pakati pa anthu, koma zimatengera nyansi kuti moyo utulukemo. Amen!

⁹⁶ Pokhapokha chirichonse chitafa ndi kuvunda, moyo sungatulukemo mwa icho. Pokhapokha munthu atafa ndi kuvunda mmaganizo mwake momwe, Khristu sangalowe mumtima mwake. Pamene iwe ukuyesetsa kuti udziganizire wekha, "Tsopano, ngati ine ndingayende kupita pa guwa ndi kukati, 'Inde, Ambuye, ndine—ndine munthu wabwino, ine ndikutengani Inu. Ine ndizipereka zakhumi zanga. Ine ndizichita izi,'" iwe ukuyenera kuti ufe ndi kuvunda pomwe apo ku malingaliro ako. Nkuwulola Mzimu Woyera utenge ulamuliro ndi kumangochita nawe chirichonse chimene Iye akufuna kuti azichita nawe. Kukhala ngati wanyansi ndi zimenezo. Zimenezo zikumveka zowopsya, osati kusinjirira, koma ndi Choonadi. Ndiyo njira yokhayo imene ine ndimadziwira yokhomerera chinthucho kuti ndikupangeni inu mumvetsetse Icho.

⁹⁷ Chinali nyansi mochuluka ndi chiyani kuposa gulu lolemekezeka la Ayuda lija tsiku lijali, kuposa kuwawona anthu awa akutuluka pamenepo ndi milomo yachibwibwi? Inu mukudziwa chibwibwi ndi chiyani? "Huh, huh, huh, huh, huh, huh...?..." Malirime ena, ndi kumachita ngati anthu oledzera. "Huh, huh, huh, huh, huh." Ndizo ndendende zomwe iwo ankachita. Iwo ankawoneka awuve!

⁹⁸ Ndipo iye anati, “Kodi amuna onsewa akhuta vinyo watsopano?”

Koma mmodzi atabwerera mmalingaliro ake, anati, “Mulole ichi chidziwike kwa inu, ndipo mverani mawu anga, awa sanaledzere monga inu mukuganizira kuti atero.” Koma iye anabwerera mmbuyo ku Lembu, “*Ichi* ndi *chijachi* chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli, ‘Ndipo zidzachitika mmasiku otsiriza,’ atero Mulungu, ‘Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse.’”

⁹⁹ Umo ndi momwe Mpingo unabadwira poyamba. Ndi angati amene amakhulupirira kuti Mulungu ndi wopanda malire? Ndiye Iye sangakhoze kusintha. Ndipo ngati limenelo linali lingaliro Lake la Mpingo pachiyambi, ndiwo mtundu wa Mpingo umene Iye ati adzakhale nawo kumapeto. Iye sangakhoze kusintha. Chotero inu mungaloweze mmalo bwanji kugwirana chanza, kapena kukonkha, kapena—kapena chinthu china chimene icho sichinachitike kumeneko? Mmodzi aliyense wa atumwi amabwerera ku chimenecho.

¹⁰⁰ Iwo atatha kuchita zonse izi. . . Mzimu Woyera unagwa pa iwo, Petro anati, “Kodi ife tingaletse madzi, powona kuti awa alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira pachiyambi?” Ndipo iye anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu. Ndiko kulondola.

¹⁰¹ Paulo anapita ndipo anakawapeza anthu akufuula, ali ndi nthawi yopambana, gulu la Abaptisti akulemekeza Mulungu, ndipo iye anati, Machitidwe 19, iye anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuyambira pomwe inu munakhulupirira?”

Iwo anati, “Ife sitikudziwa nkomwe kuti kuli Mzimu Woyera uliwonse.”

Anati, “Inu munabatizidwa chotani?”

Iwo anati, “Ife tinabatizidwa ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu, Yohane M’batizi.”

¹⁰² Iye anati, “Eya, izo sizigwiranso ntchito.” Mukuona? Petro anali atasindikiza kale izo pa Tsiku la Pentekoste. Iye anali ndi fungulo. Mukuona?

Anati, “Izo sizigwira ntchito panonso, inu muyenera kuti mubatizidwensho kachiwiri.” Chotero iye anawabatizanso iwo kachiwiri, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Anaika manja ake pa iwo, ndipo iwo anali ndi zotsatira za mtundu womwe womwewo zomwe iwo anali nazo uko pachiyambi. Mzimu Woyera unadzagwa pa iwo, iwo anayamba kuyankhula mmalirime ndi kunenera.

¹⁰³ Tsopano, umenewo wakhala uli Mpingo kudutsa mu m’badwo. Tsopano, izo zinayambira pomwe apa pachiyambi.

“Ine ndikudziwa chipiriro chako. Ndiwe woleza mtima, Ine ndikudziwa zimenezo. . . Tsopano kumbukirani, Ine ndine Iye

amene akuyenda pakati pa zoyikapo nyali. Ine ndikudziwa chipiriro chako, ndi ntchito yako, ndi kulimbika kwako, ndi chikondi chako, ndi zina zotero. Ine ndikudziwa zonse zomwe iwe wachita. Ndipo ndikudziwa kuti iwe wawayesa anthu awa omwe akudzitcha okha 'aneneri, atumwi,' ndipo wawapeza kuti iwo ndi abodza." Oh, uko nkusapsyatira basi, sichoncho izo? Ine ndiribe chochita pa izo, ndi Iyeyo. Iye anati iwo ndi abodza.

¹⁰⁴ Koma Baibulo linati, "Muyeseni munthu. Ngati pali wina pakati panu amene ali wauzimu kapena mneneri, kapena akunena kuti iye ali, Ine Ambuye ndidzazizindikiritisa Ndekha kwa iye. Ine ndidzayankhula naye mmasomphenya, ndi mmaloto. Ndipo ngati chimene iye anena chidzachtika, ndiye mudzamumvere iye; musadzachite naye mantha, mwaona, chifukwa chakuti Ine ndiri naye. Koma ngati izo sizidzachtika, ndiye musadzamumvere iye, iye alibe Mawu Anga." Mwawona, ngati ali Mawu Ake, izo zidzachtika.

¹⁰⁵ Tsopano, iwo anapeza kuti anthu awa samachita molingana ndi Baibulo. Mwaona, iwo anali kuyesetsa kuti apeze china chakenso. (Ine ndikufuna kuti inu musunge chipewa chanu choganizira tsopano, ife tikamatsikira ku chonona mu maminiti pang'ono chabe.) Tsopano, ndiye Iye anati, "Ine ndikuwona chimene iwe uli...kuti iwe uli ndi kuleza mtima, ndi chipiriro,...ndi iwo. Iwe wawayesa iwo, ndipo wapeza kuti iwo siali atumwi. Iwo siali."

¹⁰⁶ Tsopano, monga ine ndinanenera poyamba, ife tisanayambe pa izi, chitsitsimutso chirichonse chimabala mapasa awiri. Wina amakhala munthu wauzimu; winayo amakhala munthu wachirengedwe wapadziko lapansi, "Ine ndinajowina tchalitchi, ndine wabwino basi monga aliyense." Ndipo ndicho chimene chitsitsimutso ichi chinabala. Ndi chimene, chitsitsimutso chirichonse. Izi ndi zomwe Luther anabereka, ndi zomwe Ireniasi anabereka, ndi zomwe Martin Woyera anabereka, ndi zomwe Columba anabereka, ndi zomwe Wesley anabereka, ndipo ndicho chimene Pentekoste yabereka. Ndendende basi.

¹⁰⁷ Inu mukuwona momwe iwo apitira ku mbewu? Amanga matchalitchi awo, ndipo apita mosochera, ndi malo abwino aakulu ndi (mai, kalanga!) amaimirira ndi kubwereza Chikhulupiriro cha Atumwi. "Ine ndimakhulupirira mu Mpingo Woyera wa Roma Katolika, ndi kuyankhulana ndi oyer." Aliyense amene amakhulupirira mu kuyankhulana ndi oyer ndi wazamizimu. Chirichonse chimene chimayankhulana ndi akufa ndi cha mdierekezi. Ndiko kulondola ndendende. Ife tiri naye mkhalapakati mmodzi pakati pa Mulungu ndi munthu, ameneyo ndi Munthu Yesu Khristu. Uko nkulondola. Ndizo zimene Petro ananena. Ndipo inu anthu Achikatolika okonededwa mumamutcha iye "papa woyamba, ndipo Petro kukhala papa woyamba amene anayenda ndi Yesu."

108 Ndiyeno iye anati, “Palibe mkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi munthu.” Ndipo awa, muli nawo ena masauzande teni lero. Nchifukwa chiyani zasintha kwambiri, ngati mpingo ndi wosalephera ndipo sungakhoze kusintha? Ndipo misa zanu zonse zimanenedwa mu Chilatini kuti izo zisasinthe. Chinachitika ndi chiyani? Kodi inu munapeza pati Kachikhulupiriro ka Atumwi mu Baibulo? Ngati atumwi anali ndi kachikhulupiriro kalikonse, kanali “Lapani, ndipo mubatizidwe aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha tchimo lanu.” Panalibe kachikhulupiriro kena kamene ine ndinawamvapo iwo akukadziwa kapena akubwereza konse kena kalikonse.

109 Koma pamene izo zifika ku “mipingo Yoyera ya Roma” ndi zinthu zina zonsezi, ndi “Mulungu Atate Wamphamvuzonse amene amasunga miyamba ndi dziko lapansi,” zimenezo ndi zamkhutu. Mukuona? Uko nkulondola. Zimenezo mulibemo mu Baibulo. Mulibemo chinthu choterocho mu Lemba. Iko ndi kachikhulupiriro kodzipangira komwe iwo anapanga. Koma ndizo...mapemphero onse ndi chirichonse ndi chinthu chopangidwa.

110 Ife tikukhoza kuwona lero kuti Achiprotestanti athu, pamene ife tinafika kumusi kuno, anangochoka kumene kwa iwo. Ndipo chimodzimodzi monga Billy Graham ananenera Lamlungu, “Anthu akhala akulakwitsa mochuluka kwambiri mpaka iwo amaganiza kuti akulondola pamene iwo akulakwitsa.” Uko nkulondola. Ichu ndi choonadi. Ndine wokondwa kuti ndine...Chifukwa ine ndikudziwa Billy Graham analandira Mzimu Woyera pansu pa George Jefferies kumeneko, koma ena a masiku awa iye adzatuluka mmenemo. Mulungu akumugwiritsa iye ntchito kumeneko tsopano, chifukwa iye akutha kugwedeza ufumu umene palibe wina aliyense amene akanatha kukalowamo. Koma inu mutha kuwona kulalikirira kwake, kuti kuli chinachake kuseri kwake, chifukwa cha ena mwa awa pano Achibaptisti ogwirana chanza. Inde, bwana!

111 Tsopano:

Ine ndikudziwa ntchito zako, . . . ndi chipiriro chako, . . . momwe kuti iwe sungathe . . .

112 Tiyeni tiwone tsopano, ine ndapeza . . .

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi kulimbika kwako, ndi chipiriro chako, . . . momwe iwe sungakhoze kupirira nawo iwo amene ali oyipa: ndipo wawayesa iwo amene akunena kuti ali atumwi, koma iwo siali, ndipo wawapeza iwo kuti ndi abodza:

113 Iye anawapeza iwo kuti ndi abodza. Iwo anadziwa bwanji zimenezo? Iwo samabwereza powerenga Mawu.

114 Tsopano, ngati munthu anena kuti “Baibulo ili limanena mu Ahebri 13:8, ‘Yesu Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,’” munthuyo nkuti, “Ah, masiku a zozizwitsa anapita,” ndiye kuti munthu ameneyo ndi wabodza.

115 Ngati Baibulo linati, “Lapani, ndipo mubatizidwe aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu ku chikhululukiro cha machimo anu,” ndipo malo aliwonse mu Baibulo nkumanena chinthu chomwe chomwecho, ndipo aliyense amene anabatizidwapo mu—mu nthawi ya Baibulo ankabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo iye anawatuma iwo kuti azikabatizidwa, kukonkedwa, kapena chinachake chonga chimenecho, munthu ameneyo ndi wabodza, wapezeka kuti ndi mneneri wabodza.

116 Ine ndikudalira kuti sindikuvulaza kumverera kwanu, koma ine. . . M’bale, inu—inu simungathe kusasatitsa Izi, ndi nthawi yake, chotsani magolovesi ndipo mugwire Uthenga. Mukuona? Ndicho Choonadi.

117 Tsopano, ndiwonetseni ine china chosiyana. Ndiwonetseni ine pamene munthu mmodzi anabatizidwapo mwanjira ina iliyonse kupatula mu Dzina la Yesu, mwawona, kunja kwa mpingo wa Katolika. Chotero ngati inu munabatizidwa mwanjira imeneyo, inu simuli mu mpingo wa Chikristu, inu muli mu mpingo wa Katolika chifukwa inu munabatizidwa. *Sunday Visitor* yawo yomwe, katekisima inati, funso, “Kodi wa Chiprotestanti aliyense adzapulumutsidwa?” Anati, “Ambiri a iwo, chifukwa iwo ali ndi ubatizo wathu ndi zinthu zambiri monga choncho.” Anati, “Iwo amadzinenera za Baibulo, ndipo Baibulo linati ‘muzibatiza mu Dzina la Yesu Khristu,’ ndipo tazitenga izo kuchokera pamenepo ndipo tinaikapo ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera’ ndipo iwo agwera pansu kwa izo.” Ndithudi. Mukuona? Osati—osati. . . Si a—si ubatizo wa Chikristu, ndi ubatizo wa Chikatolika.

118 Kodi inu munandimva ine usiku, “Kodi inu munabatizidwapo mu ubatizo wa *Chikristu*?” Ubatizo wa *Chikristu*, Khristu, “Yesu Khristu,” osati mu udindo wina.

119 Tsopano, ndime ya 3 tsopano. Chabwino, ndime ya 2 ndi ya 3. Tsopano ndime ya 3:

Ndipo walola, ndi kukhala ndi chipiriro, ndipo chifukwa cha dzina langa walimbikira, ndipo sunakomoke ayi.

120 “Chifukwa cha Dzina Langa.” Kodi inu munazindikira kuti iwo anali ndi chipiriro? Anavutikira chiyani? Dzina Lake. Mukuliwona Dzina limenelo likukhazikika mu mpingo umenewo? Tsopano penyani izi, pamene ife tizidutsa msabatayi, momwe izo zikuzimiririra ndi kupita mu dzina lina. Mukuona? “Wakhala ndi chipiriro, kuvutikira, ndi zina zotero, ndi chifukwa cha Dzina Langa.” Iye. . . Iwo anavutikira Dzina Lake, kuti

asunge Dzina la Yesu Khristu pamwamba pa mpingo uliwonse, pamwamba pa china chirichonse.

¹²¹ Kulola kuti Ilo likhale loyambirira mu, “Chirichonse,” Baibulo linati, “chirichonse chimene mungachite mu mawu kapena mu ntchito, chitani izo zonse mu Dzina la Yesu Khristu.” Nkulondola uko? “Chirichonse chimene mungachite mu mawu kapena mu ntchito.” Ngati inu mukukwatitsa, muzimkwatitsa munthu; ngati inu simungathe, ngati iwo onse asokonezeka muukwati wawo, musawakwatitse iwo konse. Mukuona? Ngati inu simungathe kunena momasuka, “Ine ndikuluengezani inu mwamuna ndi mkazi mu Dzina la Yesu Khristu,” asiyezi iwo azipita. Chabwino. Ngati inu mukufuna kuwabatiza iwo, abatizeni iwo mu Dzina la Yesu.

¹²² Ngati inu mukuyenera kuchita chinachake chimene inu simungathe kuchita mu Dzina la Yesu, zisiyeni izo zokha! Winawake akati, “Imwani chakumwa pang’ono.” Inu simungachite izo mu Dzina la Yesu, chotero zisiyeni izo zokha! Winawake akati, “Sewerani makadi pang’ono.” Inu simungachite izo mu Dzina la Yesu, chotero zisiyeni izo zokha! Nthabwala pang’ono, yonyansa, yamanyazi pa phwando lanu la mlatho, inu simunganene zimenezo mu Dzina la Yesu, chotero zisiyeni izo zokha! Mukuona? Inu simungathe kuvala makabudula mu Dzina la Yesu, chotero zisiyeni izo zokha! Ine ndikhoza kumangopitirira, koma ife. . . inu mukudziwa zomwe ine ndikunena. Chabwino. Inu simungachite zimenezo. Zomwe simungathe kuchita mu Dzina Lake, zisiyeni izo zokha! Chifukwa, Iye anati, “Chirichonse chimene mungachite mu mawu ndi mu ntchito, muchite izo zonse mu Dzina la Yesu Khristu.” Chabwino, tsopano.

¹²³ Tsopano ife tikupita ku. . . Ndizo. . . Iye anawayamikira iwo chifukwa cha izo. Tsopano ine ndikamba za chodandaula tsopano mu mutu wa 4. . . kapena ndime ya 4, kani.

Koma ndiri nako kanthu kotsutsana ndi iwe, chifukwa iwe unataya chikondi chako choyamba.

¹²⁴ Oh! “Ine ndiri ndi kanthu kotsutsana nawe. Iwe wakhala wopirira, iwe wagwiritsitsa Dzina Langa.” Kodi icho sichingakhale chinthu chabwino basi cha kachisi uyu lero? Inde, bwana! “Iwe wakhala wabwino bwino, ndipo wakhala ndi chipiroro chambiri, ndipo wapirira nthawi yayitali, koma chinthu chake ndi ichi. . . Iwe wagwiritsitsa Dzina Langa. Ine ndikuyamikira zonse zimenezo. Ine—ine ndikukuyamikira iwe chifukwa cha zimenezo, ziri bwino. Ndipo ine ndawona kuti iwe wawayesa iwo omwe amati iwo ndi atumwi ndi zina zotero, ndipo wawapeza kuti iwo ndi abodza, iwo sakugwirizana ndi Mawu. Ine—ine ndikuyamikira izo zonse. Koma pali chinachake chimene Ine ndiri nacho chotsutsana nawe, ndipo icho ndi chakuti iwe unasiya chikondi chako choyamba. Iwe unasiya chikondi chija chomwe unkakhala nacho pa misonkhano

yabwino ija, yachikale, ya Mzimu Woyera, ndipo ukuyamba kuseserekerera mmbuyo kukalowa mu zofunda zimenezo, kumalowamo ndi 'Atate wathu . . .'" Zamkhutu! Mukuona?

¹²⁵ Gulu lonse ili apa, ndipo wina ayenera kutulukira atavala mwinjiro waukulu pa iwo (inu mukudziwa, kuti akayimbe mu kwaya, inu mukudziwa), ndipo atazipentapenta tsitsi lawo lonse ndi chirichonse, ndi zodziphoda zambiri pa nkhope zawo, ndi kumayimba monga ngati ine sindikudziwa chiyani.

¹²⁶ Kuno osati kale kwambiri, ngati pakanapanda kukhala msonkhano wa Oral Roberts, ine ndikutsimikiza ndikanalitulutsitsa gululo panja. Ine ndinali—ine ndinali pa msonkhano wa Amuna Azamalonda ndipo iwo unkachitikira . . . ife tinalibe . . . usiku umenewo ine ndinali woti ndiyankhule. Iwo sakanachitsira iwo kumeneko mu hotelo, ndipo iwo ananditengera ine ku—ku nyumba ya Oral Roberts. Ndipo pamene ine ndinali nditakhala mowerengera mwa Oral, panali gulu la ana Achipentekoste (oh, anyamata ndi atsikana, sikisitini, usinkhu wa zaka seventini, eyitini) onse atayima kunja uko; pafupifupi sarte kapena forte a iwo amati ayimbe mtundu wina wa—wa pang'ono . . . zimamveka kwa ine ngati mtundu wina wa kugwedeza kwa winawake wonga yemwe Becky amamukamba, Tchaikovsky kapena mtundu wina wa zinthu monga choncho; ine sindikudziwa, nyimbo za mtundu wina ngati zimenezo, nyimbo zachikale. Ndipo apa iwo anali, abale anali oti akukatenga chopereka mu msonkhano, ndipo mmodzi aliyense wa awa amatsatira kumeneko ndipo anali ndi chotengera chaching'ono chija, kumachita ngati iwo anali akhungu ndi nthabwala zonse ndi kumapitirira zomwe inu munazimvapo, pakati pa anyamata ndi atsikana awo, ndi kumayankhula ngati chirichonse. Ndipo atsikana amenewo ali ndi penti yokwanira pa iwo, akanatha kupaka nyumba ya Oral, pafupifupi. Ndipo pamenepo iwo anali monga chomwecho, ndi kumadzitcha okha "Apentekoste." Iwo anataya chikondi chawo chapachiyambi!

¹²⁷ Ine ndikutsimikiza ndikugwirizana ndi David duPlessis, "Mulungu alibe zidzukululu." Ayi, bwana! Ife tiri ndi zidzukululu za Methodisti. Ife tiri ndi zidzukululu za Baptisti. Ife tiri ndi zidzukululu za Chipentekoste. Koma Mulungu alibe chirichonse! Ndinu ana aamuna ndi aakazi. Inu simungabwere chifukwa cha amayi anu kapena abambo anu chifukwa chakuti iwo anali amuna ndi akazi abwino, inu muyenera kulipira mtengo wofanana ndi womwe iwo anachita. Inu mukuyenera kuti mubadwe chimodzimodzi monga iwo anachitira. Mulungu alibe zidzukululu nkomwe. Ndiwe mwana wa mwamuna kapena wamkazi; kapena, sindiwe chidzukululu chachimuna, ndicho chinthu chimodzi chotsimikizika.

¹²⁸ Tinapita ku msonkhano kumeneko, ndipo iwo kumeneko . . . ku mpingo wabwino wa Pentekostal Assembly. Mnyamata,

iwe ukanawawona akazi amenewo akubalalika pamene iwo anandiwona ine ndikulowa; ali ndi tsitsi lalifupi limenelo, lodulidwa, ndi aang'ono awo atavala mwatheka, ngati kanyimbi pafupifupi, inu mukudziwa, atafinyiridwa mkati mu madiresi amenewo monga choncho, akazi Achipentekoste, atavala mwadama kwambiri.

¹²⁹ Inu mudzayenera kuti mudzayankhire pa izo, Tsiku la Chiweruzo. Inu mudzakhala ndi mlandu wochita chigololo, Yesu anati, “Aliyense amene ayang’ana pa mkazi ndi kumusirira iye, wachita naye kale chigololo mumtima mwake.” Ndipo ngati inu mumadziwonetsera nokha kwa mwamuna monga choncho, ndani ali wolakwa? Inu kapena mwamunayo? Longosokani! Pewani mawonekedwe amene a choyipa! Mukuona? Chotero ndi zimenezotu.

¹³⁰ Kodi inu munatani? Anataya chikondi chawo *choyamba*. Oh, simungakhoze kuwaika iwo pa ngodya ndi nkhotcho kuti aziwomba mmanja mwawo ndi kumamupembedza Mulungu. Oh, ayi! Iwo akhoza kuyimba mtundu wina wa zapamwamba ndi gulu la mikanjo powazungulira iwo. Mwaona, iwo anataya chikondi chawo *choyamba*. Ndiro limene liri vuto ndi mpingo woyamba. Mukuona?

¹³¹ Iwo akuyenera basi kuti azichita monga dziko. Iwo akuyenera kuti azivala monga dziko, aziwoneka monga dziko, azichita monga dziko. Ndipo azikhala ndi katswiri wawo wokonedwa wa pa televizioni, inu mukudziwa, iwo sangasiye kuwonera zimenezo. *Ife Timakonda Susie* kapena chinachake chimzake, inu mukudziwa, iwo basi amangoyenera kuwonera zimenezo. Iwo amakhala pakhomo kujomba ku msonkhano wa mapemphero ndi china chirichonse kuti aziwonera zimenezo. Ngati iwo satero, iwo amamupatsa m’busa wawo zomutopetsa zabwino, kuti awatulutse iwo nthawi yabwino poyembekezera kuti pulogalamu imeneyo ibwere kuti akhoze kupita kunyumba akawonere zimenezo. Chikondi cha dziko lapansi kuposa chikondi cha Mulungu!

¹³² Oh, ofunda kwambiri, iwo sanganene kuti, “Ameni!” aponso. Mai, kalanga, izo zikhoza kuchotsa zodziphoda zina. Mukuona? Iwo alibenso Ilo aponso. Ndiyo Pentekoste. Imeneyo si Baptisti. Iwo sanayambe akhalapo nalo Ilo kuyamba ndi kuyamba, a—Apresbateria. Ine ndikuyankhula za Pentekoste. Uko nkulondola. Ine ndikudziwa kuti izo nzodwalitsa kwambiri, m’bale, koma ife tikufuna kubadwa kuchokera mu chinthu ichi; ziyenera kubweretsa imfa inu musanakhale ndi kubadwa. Mukuona? Mukuona? Ndicho Choonadi. Koma ndizimenezotu, munasiya chikondi chanu choyamba. Ine . . .

¹³³ Ngati Mulungu anali ndi chotsutsa chimenecho pa mpingo *uwu*, Iye ali nacho icho chowutsutsa *iwo* panonso! “Chifukwa iwe unasiya chikondi chako choyamba, Ine ndikutsutsana nawe iwe. Ine ndiri nacho chinthu chotsutsana nawe, ndicho

chodandaula Changa. Nthawi ina munkakhala ndi nthawi yopambana, koma inu—inu munalola kuti dziko liyambe kukwawiramo, ndipo munayamba kumachita mwamwambo pang'ono. Inu mukugwiritsitsabe Dzina Langa, ndipo inu mukuchitabe zinthu zomwe ziri zolondola, ndipo inu muli nacho chipiriro chochuluka ndi zina zotero, ndipo mukuvutikira, inu muli ngati mphongolo, inu mukungovutikira ndi kumagwira ntchito.”

¹³⁴ Mai! Mai! Mai! Onani, mwasiya chisomo ndi chikhulupiriro ndi mphamvu, mwazisinthanitsa izo ndi kugwira ntchito ndi zintchito. “Chabwino, ine ndikukuuzani inu M'bale Branham, ine—ine ndimathandizira mkazi wamasiye aliyense amene ine ndingathe.” Chabwino, chimenecho ndi chinthu chabwino, ine ndikukuyamikirani inu chifukwa cha zimenezo. Koma chiri kuti chikondi choyamba chija chimene iwe unali nacho poyamba? Uh-hum, uh-hum. Chiri kuti chisangalalo chija chimene iwe unali nacho? Monga Davide nthawiyina anafuula, “O Ambuye, bwezeretsani kwa ine chimwemwe cha chipulumutso changa.” Ili kuti misonkhano yamapemphero ya usiku wonse ija, ndi misozi pamasaya anu? Mai, kalanga, mpaka Baibulo likumachita fumbi ndi akangaude pa Ilo. Inu mukumawerenga nkhani zachikondi za kale, ndi nkhani ndi zinthu; ndi zinthu zomwe siziyenera kuloledwa kuti zisindikizidwe ndi kukaikidwa kugulu za—chidebe cha zinyalala, ndipo ife anthu Achipentekoste timakazitenga zimenezo ndi kungoziwunjirira izo ngati gulu la ntchentche pa chidebe cha zinyalala. Uko nkulondola. Oh, chifundo! Chimene ife tikusowa ndi: Tibwerere ku chikondi chathu choyamba! Tibwerere ku Pentekoste! Oh, ine kulibwino ndichokeko kumeneko. Chabwino. Koma, inu mukumvetsetsa, “Kusiya chikondi choyamba chija.”

¹³⁵ Ndime ya 4, ndime ya 5 tsopano. Chenjezo, ndime ya 5, chenjezo: “Kumbukira ndipo ulape!” Mukuona?

Chotero kumbukira kumene iwe wagwerako, . . . (Kodi iwe unachokera kuti? Kuyambira pa pentekoste iwe unagwera pansu pomwe iwe uli tsopano, wabwerera mmbuyo). . . ndipo lapa, ndipo uchite ntchito zako zoyambirira; (ubwerere ku pentekoste kachiwiri). . . kapena ukapanda kutero Ine ndidzabwera kwa iwe msanga, ndipo ndikachotsa choyikapo nyali mu w-a-k-e. . . (Mwaona yemwe iye ali, sichoncho inu?). . . malo ake, pokhapokha iwe utalapa.

¹³⁶ Mwakulankhula kwina, ngati inu muli ndi m'busa wodzazidwa ndi Mulungu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo inu mukuyesera kumufinyira iye pansu pa chala chanu, ndikuti, “Chabwino, ngati iye ati anene chirichonse chokhudzana ndi ife kuti tizikhala ndi kwaya yovala mikanjo, ngati iye ati anene chirichonse chokhudzana ndi ife kudziphoda, ife tingomuchotsapo iye.” Inu musadandaule, Mulungu azichita

izo inu musanapeze mwayi woti mutero. Iye adzapita kunja ndipo azikalalikira kwa miyala mu msewu iye asanayambe kumasasatitsa zinthu za mtundu umenewo. Inu mukakhala ndi m'busa amene amakuuzani inu Choonadi kwenikweni, inu mukuyenera kulemekeza Mulungu ndi kukhala mu Mzimu, ndi kumamupembedza Mulungu, kumazindikira kuti inu mutaika ngati inu simutero. Mukuona?

¹³⁷ Koma anthu akumakhala moyo lero ngati kuti... ichi ndi chinthu chokhacho chomwe chinalipo, “kukhala pano padziko lapansi, ndizo zonse.” Inu simukuzindikira kuti inu muli ndi solo yomwe iti idzacho kuno ndikudzapita kwinakwake. Ndipo inu mumasindikiza komwe inu mukukafikira komwe kuno, momwe inu mumakhalira moyo ndi momwe inu mumachitira, kumasunga mangawa, ndi kuyipidwa, ndi chirichonse, ndipo kenako nkuthamangira ku tchalitchi. Oh, chifundo! Psyi! Manyazi pa inu.

¹³⁸ Inu mumabweretsa chitonzo pa—pa cholinga cha Khristu. Kodi uko sikulondola? Kodi ife sitikumachita zimenezo? Zidakhwa sizikuwuvulaza Mpingo; sichoncho *izo*. Si hule lomwe likuvulaza Mpingo. Ndi anthu omwe amadzinenera kuti ndi Akhristu amene akuvulaza Mpingo. Ife tikudziwa chomwe chidakhwa chiri ndi chimene hule liri. Pamene alongo athu avala ngati wachiwerewere, ndi zosiyana, *izo* ndi zomwe zimavulaza Mpingo. Pamene bambo amwa ngati chidakhwa, chabwino, ndiye, ndizo zomwe zimavulaza Mpingo. Iwo akumadzinenera kuti ndi Akhristu ndipo iwo akumachita zimenezo. Anthuwo amakufunani inu amene mumatchula dzina... “Muloleni iye amene amatchula Dzina la Yesu Khristu achoke kwa tchimo.” Mukuona? Chokaniko kwa ilo.

¹³⁹ Oh, ndife operewera kwambiri, abale. Ine, inu, tonse a ife, ndife—ndife operewera kwa zomwe Khristu akufuna kuti ife tikhale. Ndipo pomwe apa mu tsiku lino ndi nthawi yoti tiike pambali tchimo lirilonse limene silimachedwa kutifooketsa ife, ndipo tithamange ndi chipiriro mpikisano umene waikidwa patsogolo pathu. Alaliki, ndiko kulondola, abale. Ndiko kulondola ndendende.

¹⁴⁰ “Kumbukirani ndipo mulape, apo ayi Ine ndichotsa Kuwala kwa nyenyeziyo pa malo pake.” Malo ake ndi ati? Mu Mpingo. “Koma ngati inu simulapa ndikubwerera komwe inu munalii pa chiyambi, Ine ndidzamuchotsa m'busa wanu kwa inu nthawi yomweyo ndi kumuchotsa iye pamalo ake; Ine ndidzakamuika iye kwinakwake komwe ake... kumene ine ndizikawonetsera Kuwala Kwanga komwe kuzikawala.” Hmm! Kodi izo sizinali zaulemu?

¹⁴¹ Yakwana nthawi yoti mipingo ilape. Yakwana nthawi yoti Pentekoste iwachotse ophunzira ambiri opukutidwa pang'ono kuwachotsa pa maguwa, ndi kutengeramo mlaliki wa kachitidwe kachikale mmenemo yemwe adzakuuzeni inu Choonadi; osati

kumangosisitana ndi kumagwiritsa ntchito tchalitchi ngati tikiti yodyera, malipiro aakulu, ndi chinachake monga choncho, ndi kuwerenga maganizo, ndi mipikisano ingapo ya akavalo, ndi maphwando a msuzi, ndi china chirichonse. Yakwana nthawi yobwereranso ku Uthenga. Ine sindikusamala kuti ndinu wochepe bwanji, “Kumene awiri kapena atatu asonkhana, Ine—Ine ndidzakhala pakati pawo.”

¹⁴² “Lapani, kuwopa kuti Ine ndisabwere ndikudzachotsa choyikapo nyali; kumutumiza iye kutali, kwinakwake akawalitseko nyali yake.”

Tsopano ndime ya 6. Tsopano apa pali yomwe tikhale nayo vuto. Tsopano, pokhapokha iwe ulape, Iye adzabwera ndikudzamuchotsapo m'busayo.

Koma izi iwe uli nazo, . . .

¹⁴³ Tsopano, kumbukirani. Oh, musati muphonye izi tsopano. Izi zitsekera zina zonsezo pamodzi, kulunjika kutsikira mpaka kwa uwu umene. . . m'badwo umene ife tirimo tsopano. Aliyense akumverera bwino, choyambirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi inu mukufulumira? [Osonkhana akuti, “Ayi.”] Chabwino, tsopano. Chabwino, mungopirira pang'ono pokha ndiye. [M'bale akuti, “Mukhale usiku wonse.”] Tsopano. . . Zikomo inu.

Koma izi iwe uli nazo, (Iwo anali ndi chinachake pamenepo, sichoncho iwo? Tsopano, kodi iwo anali ndi chiyani?) kuti iwe ukudana nazo ntchito za Chinikolai, zomwe Inenso ndikudana nazo.

¹⁴⁴ “Iwe ukudana nazo ntchito zija za Chinikolai.” Nditakhala mowerengera lero kumtunda uko, ine ndinalemba chinachake apa pa zimenezo, ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwatcheru tsopano, izo ziri pa masamba angapo apa. Ndime ya 6, mayamiko ndi kuvomereza; ndicho, Mulungu ndi Mpingo akugwirizana pa chinthu chimodzi, kuti iwo “amadana ndi ntchito za Chinikolai”; Mpesa woona, Mpesa woona, Mpingo woona umene unali mu mpingo wa Efeso uwu.

¹⁴⁵ Tsopano, kumbukirani, mpingo uliwonse umakhala ndi zofunda zake ndipo mpingo uliwonse umakhala ndi zauzimu zake. Ndiwo mapasa omwe amabadwa mu chitsitsimutso chirichonse ndipo amakhala mu mpingo uliwonse. Iwo anayamba bwino mu m'badwo *uwu* ndipo akuthera mu m'badwo *uwu*. Ndipo potsiriza, miyamboyo inadzatenga malo mu M'badwo wa Tiyatira, ndipo Luther anadzazitulutsanso izo kachiwiri. Ndipo tsopano izo zikubwereranso momwemo kachiwiri. Kodi inu mukutha kuwona chipembedzo chamwambo chimenecho? Palibepo kusiyanana pakati pa zimenezo ndi Chikatolika. Zonsezi ndi chinthu chimodzi. Bungwe lililonse likuphedwera momwemo. Mulungu sanapangepo konse bungwe Mpingo Wake. Ndizo ndendende zomwe iwo anali kuyesetsa kuti

azichita apa. Ndipo inu muyang'ane ndipo muwone tsopano ngati izo siziri zolondola, kungokuwonetsani inu momwe bungwe liriri lotembereredwa. Izo zinali—izo zinali zachirendo kwa Mpingo watsopano, Mpingo wa Chipangano Chatsopano. Mukuona?

Koma... iwe... Koma ichi iwe uli nacho, kuti iwe ukudana nazo ntchito za Chinikolai, zomwe Inenso ndikudana nazo.

¹⁴⁶ Mpesa woona unkadana nazo ntchito zamwambo za Chinikolai, Mulungu amateronso. Zomwe zinali ntchito mu mpingo wa Efeso, mu mpingo wa Efeso, zinadzakhala chiphunzitso mu mpingo wa Pergamo. Mu Efeso, mpingo woyamba, izo zinali ntchito, mu mpingo wotsatirawo izo zinadzakhala chiphunzitso. Kodi inu mukukhoza kuzimvetsa izo? Kodi inu mukukhoza kuzimvetsa izo tsopano? Izo zinali ntchito mu Efeso, ndipo penyani, cha kuno mu Pergamo icho chinadzakhala chiphunzitso. Icho chinangoyamba apa mwa mawonekedwe akhanda. Tsopano, mu miniti ife tipeza chomwe icho chinali. Apa pali *mimbulu* ya Paulo, “ntchito za Anikolai.”

¹⁴⁷ Tsopano chiyani... Tiyeni tiwaswe mawu amenewo ndi kupeza zomwe ife tiri nazo ife tisanapite patali. Mawu akuti *Chinikolai* ndi chinthu chachirendo kwa ine. Ine ndiri ndi la lexicon la Chigriki lililonse limene ine—ine ndikanakhoza kulipeza. Chinikolai limachokera ku mawu a *Nicko*, N-i-c-k-o. Dikirani, ine ndikukhulupirira ndinalemba izi apa. N-i-c-k-o, *Nicko*, zomwe zikutanthauza “kugonjetsa kapena kulanda.” *Nico-laitane*, “kulanda kapena kuwagonjetsa anthu wamba.” Zomwe iwo amayesetsa kuti achite apa zinali kuyesetsa kuwutenga mpingo kumene Mulungu anali ndi azibusa, ndipo Mzimu wa Mulungu ukuyenda mwa mphatso mu Mpingo wa Mulungu wamoyo, ndipo, iwo anali nako kuyamba kwa chiphunzitso chimene iwo akanadzakhala ndi ansembe ena, ndi mabishopu, ndi mapapa, ndi zina zotero. Zimenezo, Mulungu anati, Iye amadana nazo! Iye akudana nazo apobe lero. *Nico-laitanes*, (*Nicko*, “kugonjetsa”) kapena, “kuwalanda anthu wamba.” *Anthu wamba* ndi “mpingo.” Ndi angati amadziwa kuti anthu wamba ndi mpingo? Chabwino, “Kuwalanda kapena kugonjetsa, kapena kutenga malo a anthu wamba.”

¹⁴⁸ Mwakulankhula kwina, kukuchotsa kupatulika konse, mphamvu zonse kuzichotsa kwa mpingo, ndi kukaziyika izo pa ansembe; “Kuwasiya osonkhana kuti azikhala moyo momwe iwo akufunira, koma wansembe ndiye woyerayo.” Kuwuchotsa Mzimu Woyera kwa anthu ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwatsatira iwo, ndi kuzichotsapo izo ndi kuwapatsa iwo unsembe woyera. Kuchotsapo Mzimu Woyera ndi kusinthanitsa Iwo ndi unsembe. Inu mukuwona chimene izo zinali? Izo zinali... Icho potsiriza chinadzakhala... Mu mpingo *uwu* kuno, izo zinali ntchito; ndipo malo *awa* icho

chinadzakhala chiphunzitswo; ndipo Tiyatira, iye anadzazitenga izo. Ndipo pamene Luther anadzatulukira, iye sakanakhoza kukhala mwanjira imeneyo, iye anabwerera mmbuyo ndipo anadzazilandanso kachiwiri: mabishopu, makardinolo, mabishopu aakulu. Ndi ndani mu dziko amene ali mutu wa Mpingo wa Mulungu kupatula Iye Mwiniwake? Ameni! Psi! Tsopano ine ndikumverera mwachipembedzo. Mzimu Woyera unatumizidwa kuti uzidzalamulira Mpingo; osati mlaliki yekha, osonkhana onse! . . . mlaliki yekha akhale woyera, ndi, Mpingo wonse uli nawo Mzimu Woyera.

149 Ndipo mmalo mwa Iwo, mmalo mokhala ndi Mzimu kuti uzipanga zimenezo, iwo atenga kokulumunya kakang'ono ndi bisiketi, ndi vinyo wina, ndi kumadzitcha izo "*Ukaristia* woyera zomwe zimatanthauza 'Mzimu Woyera.'" Zingatheke bwanji mdziko kuti bisiketi ndi chidutswa cha vinyo zikhale mzimu? Tsopano, ngati—ngati njira yake ndi imeneyo, inu muyenera kuweringa Machitidwe 2 motere: "Pamene tsiku la Pentekoste linafika kwathunthu, apa panadzabwera wansembe wa Chiroma tsidya la msewu, ndipo iye anati "Tulutsani lirime lanu" ndipo iye anadzayika kokulumunyako pamenepo, ndipo anadzamwera vinyo, anati, "Tsopano inu mwalandira Mzimu Woyera." Tsopano, tsopano ife tikuganiza kuti izo ndi zowopsya. Ndi choncho.

150 Tsopano tiyeni titsikire mmusi; ine ndinadzozedwa mu mpingo wa Baptisti, tiyeni titenge ife Abaptisti. Uh-nhu. Hmm? Amethodisti, kodi ife timachita chiyani? "Ngati inu mungavomereze kuti 'Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu,' inu mwapulumutsidwa." Mdierekezi amakhulupirira kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu, ndipo amanjenjemera pa Izo; mwinamwake amakhulupirira izo kuposa momwe mamembala ambiri a mpingo amachitira. Mdierekezi amakhulupirira chinthu chomwe chomwecho ndipo amanjenjemera, chifukwa iye amadziwa kuti iye wathedwa.

151 Tsopano ife tizitenge izo mmawonekedwe a Methodisti, iwo—iwo amanena kuti "Yohane sankabatiza," kuti, "iye ankakonkha." Anati, "Kunali makoswe ambiri mdzikolo, ndipo—ndipo madzi ankatuluka kuchokera mmalo. Ndipo iye anali ndi chigoba cha nkho ndipo anakumba dzenje la khoswe." Ndipo iwo amalalikira zimenezo kwenikweni. "Ndipo amakhala ndi madzi ena mu chigoba cha khoswe ichi, kapena chigoba ichi cha nkho, kuchokera mu dzenje la khoswelo, ndipo ankawakonkha anthu." Zamkhutu! Oh, m'bale!

152 Chabwino, apa ife titenga izo, "Pamene tsiku la Pentekoste linadzafika kwathunthu, iwo onse anali pamalo amodzi, mogwirizana. Ndipo abusa anabwera kumeneko ndipo anadzalalikira ulaliki wabwino, ndi kuti, 'Ndipatseni ine dzanja lamanja la chiyanjano, ndipo tilemba dzina lanu mu bukhu.'" Izo sizikumveka bwino, zikutero izo? Inu mukhoza kuzimvetisa

izo. . . Inu simungathe kuzipeza izo mu almanac, iwo ankadziwa bwino kuposa zimenezo. Old *Ladies Birthday Almanac* ndi yolondola kwambiri kuposa momwe izo zingakhalire.

¹⁵³ Chabwino, nchiyani chinayambitsa zimenezo, ndiye? Anikolai anabweretsa gulu la amuna kuti likapotoze Lemba, ndi kudzapanga chipembedzo chimene sichingalole Mulungu kuti aziyendamo. Amafera pomwepo! Ndiye Iye anati apa, “Inu mwafa! Inu muli nalo ‘dzina’ inu muli wamoyo, koma ndinu wakufa!” Ambiri a iwo, anafa, ndipo sakudziwa izo.

¹⁵⁴ Ine ndi mchimwene wanga tinali kuwedza, ife tinali anyamata aang’ono, kumtunda kuno. Ndipo ine ndinagwira kamba wokalamba, ndipo ine ndinamudula mutu wake; ndinamuchotsapo iye pa chingwe, sindinafune kuti ndipusitsike ndi chinthu chimenecho; ndipo ndinamuponyera iye pa gombe kumeneko. Ndipo mchimwene wanga wamng’ono anabwera, ndipo iye anati, “Kodi iwe unagwira chiyani kanthawi kapitako?”

Ine ndinati, “Kamba.”

Iye anati, “Kodi iwe unachita naye chiyani iye?”

Ine ndinati, “Apo, ali apoyo, *pamenepo*, ndipo mutu wake uli *pamenepo*.”

Ndipo iye anapita kumeneko. Ndipo iye anati, “Kodi iye wafa?”

Ine ndinati, “Ndithudi! Ndinalakanitsa mutu wake ndi thupi lake, iye ayenera kuti wafa.”

¹⁵⁵ Chotero ndiye iye anatenga ndodo, ndipo anayamba kufikira pansu kuti aponyere mutu wa kamba uyu kubwerera mu mtsinje, ndipo pamene. . . kapena kakhwawa. Ndipo pamene iye anatero, kamba wakaleyo anaigwira iyo. Inu mukudziwa, iwo analimbana kwa ora limodzi kapena awiri. Iye analumphira mmbuyo, iye anati, “Hei! Ine ndimaganiza umati, ‘Iye wafa.’”

Ine ndinati, “Iye ali.”

Iye anati, “Chabwino, iye sakudziwa zimenezo. Ayi.”

¹⁵⁶ Chotero ndi momwe anthu ambiri aliri: akufa ndipo sakudziwa izo! Achinikolai! Oh, mai! Oh, Iye anati, “Iwe ukudana nacho icho.” Kumatenga ansembe athunthu, abwino oyoera, kardinolo woyera, bishopu woyera.

¹⁵⁷ Ndipo ena a inu Achipentekoste, “Woyang’anira wamkulu, kumulola iye kuti abwere kuno. Woyang’anira wamkulu, iye adzakuwuzeni inu ngati inu mungakhale ndi msonkhano wamachiritso pano kapena ayi. Ha, ha.” Aleluya! Mzimu Woyera ndi umene unganene zimenezo kapena ayi, Mawu Amuyaya a Mulungu.

¹⁵⁸ “Chabwino, M’bale Branham, ife timakhulupirira kuti Baibulo limaphunzitsa ‘mubatize mu Dzina la Yesu,’

koma woyang'anira wamkulu anati ngati ife tingayambe zimenezo mu tchalitchi chathu, iye angatithamangitsire ife tonse panja." Kazichitani zimenezo. Ndiko kulondola. Ine kulibwino ndithamangitsidwire kunja kuno kusiyana ndi kudzathamangitsidwira kunja Uko. Chotero, ngati inu mudzachotsa chirichonse *apa*, inu mudzakankhidwira kunja Kumeneko, mulimonse, chotero kuli bwino akukankhireni panja kuno. Ngati akukankhirani panja kuno, inu mudzakankhidwira mkati Kumeneko. Chotero ndizo basi chinthu chomwe chomwecho, chotero mukhale molondola ndi Iwo.

¹⁵⁹ Ife timafuna kukhala olondola. Oh, mai, ndi chinthu chovuta, m'bale. Ife tiyenera kupeza chinthu ichi molondola. Ife sitidzakhoza konse kukhala ndi Mpingo kufikira Mulungu atapeza maziko oti awuyikepo Iwo. Iye sadzamangapo Mpingo Wake pa gulu la zamkhutu. Iye akuyenera kuti abwere pa Mawu Ake kapena Iye sadzabwera konse; pa Mawu Ake omwe.

¹⁶⁰ Winawake, osati kale kwambiri, kumtunda uko, anati, "M'bale Branham, mudzabwere ku Chautauqua." Ndi angati analiko ku Chautauqua? Bwanji, tangowonani apa, gawo limodzi mwa magawo atatu a mpingo kapena kuposerapo linali ku Chautauqua. Chimene...Tsopano, bambo ameneyo anafika kumeneko masana amenewo, ndipo inu nonse munamumva iye, osadziwa kuti ine ndidziwa za zimenezo. Mulungu akhoza kuwulula mu chipinda kumtunda uko zomwe iwo akunena kumusi uko, ndipo, inu mukudziwa, Iye anachita zimenezo. Anabwera kumeneko, anati, "Tsopano, M'bale Branham, oh, iye ndi wantchito wa Ambuye. Pamene Mzimu uli pa iye, iye ndi mneneri wodzozedwa, iye ndithudi amadziwa, Mulungu amamuza iye zomwe ziri ndi zomwe ziti zidzakhale; koma fioloje yake, musati mumvetsere kwa zimenezo."

¹⁶¹ Lingaliro lobalalika bwanji limenelo! Munthu anganene bwanji zimenezo! Bwanji, ine sindinatero...Chabwino, ngati inu simumazidziwa nyemba zoswedwa kwa khofi, inu—inu mungadziwe bwino kuposa zimenezo. Inu mungaganize bwanji nkomwe za chinthu chonga chimenecho? Chifukwa chiyani? Bwanji, mawu kumene oti *mneneri* iwoeni amatanthauza "wowulula Wauzimu wa Mawu." Zingatheke bwanji inu...? "Mawu a Ambuye ankabwera kwa mneneri." Ine sindinanene kuti ndine ameneyo, iwo anatero. Koma ndi zimenezotu. Mukuona?

¹⁶² Momwe munthu, amagwirizira kachiphunzitso kakang'ono ka tchalitchi kwinakwake, chifukwa bungwe lawolo silimagwirizana nawo Iwo, kugulitsa mafulu anu obadwa ndi chipere cha mphoza, Esau, iwe wachinyengo womvetsa chisoni! Uko nkulondola. Kugulitsa kwa mafulu anu obadwa ndi chipere cha mphoza, chifukwa cha chipere cha chipembedzo, chipere cha bungwe lomwe Mulungu amadana

nalo. Ingokumbukirani, inu mukuti “bungwe,” Mulungu amadana nalo! Ndi chinthu chimene chinalekanitsa abale, ndi kuphwanyira pansi. . . Alipo ambiri a Amethodisti, Abaptisti, ndi Apresbateria, usikuuno, angakonde atakhala ndi chiyanjano pozungulira gome la Mulungu. Koma ngati iwo angatero, iwo angathamangitsidwe nthawi yoyamba yomwe iwo angayambe kulowa mu zimenezo. Ndiko kulondola ndendende.

¹⁶³ “Amayi anali a icho,” ndipo iwo angokhala chidzukulukuyamba ndi kuyamba. Oh, mai! Ine sindikusamala kuti amayi anali a chiyani, amayi anakhala mu Kuwala konse komwe iwo anali nako mu tsiku lawo, inu mukukhala mu tsiku lina.

¹⁶⁴ Sayansi inatsimikizirapo kale, pafupifupi zaka firii handiredi zapitazo, pozungulitsa mpira kuzungulira dziko lapansi, anati, “Ngati galimoto iliyonse itayenda mothamanga kwambiri liwiro la mamailosi sarte pa ora, mphamvu yokokera pansi ikhoza kuinyamula iyo kuchokera pansi ndi kuipititsa iyo mu mlengalenga.” Inu mukuganiza sayansi lero ingakhulupirire zimenezo? Iwo akumayendetsa mamailosi naintini handiredi pa ora. Iwo sakuyang’ana mmbuyo kuti awone zomwe iwo ananena, iwo akuyang’ana mmbuyo, akuyang’ana zomwe iwo angawone akamayang’ana chitsogolo.

¹⁶⁵ Koma mpingo nthawizonse umafuna kuyang’ana mmbuyo, kuwona zomwe Wesley ananena, zomwe Moody ananena, zomwe Sankey ananena. “Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira,” tiyeni tiziyang’ana chitsogolo! Chinthu chokhacho mu Baibulo chimene chimayang’ana chammbuyo. . . Kodi inu mukudziwa mtundu wanji wa chinyama chimene chimayang’ana mmbuyo nthawizonse? Moyo wotsikitsitsa umene ulipo. Ndi angati akudziwa kuti moyo wotsikitsitsa ndi uti umene umayenda? Chule. Chule ndi moyo wotsikitsitsa kwambiri umene ulipo, ndipo munthu ndiye moyo wapamwamba kwambiri umene ulipo. Ndipo chule amayang’ana chammbuyo. Ine sindimakonda moyo wakale wotsika umenewo. Ine ndikufuna ndiziyang’ana chitsogolo, ndikukhulupirira, kudalira, kumayenda mu Kuwala monga Iye ali mu Kuwala, ameni, pamene Iye akuwalitsa Kuwala.

¹⁶⁶ Nthawi ina ku Kentucky ine ndinali ndi msonkhano, munthu wachikulire anatulukira, ndipo iye anati, “Oh, sindikukhulupirira machiritso amenewo.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ziri bwino, ndinu wa Chimereka.”

Iye anati, “Ine—ine sindikhulupirira chirichonse pokhapokha ine nditachiwona icho.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ziri bwino.”

Iye anati, “Tsopano, ine ndiribe kanthu kotsutsana ndi inu, koma ine—ine sindimakhulupirira zimene inu mukunenazo.”

Ine ndinati, “Ndi ufulu wanu womwe wa Chimereka, inu simukuyenera kutero.”

Iye anati, “Tsopano, ine sindimavomereza kalikonse pokhapokha ine nditakawona bwinobwino.” Hmm!

Ine ndinati, “Chabwino, tsopano ine . . . ndizo—ndi zabwino, inu muyenera kuti mukuchokera ku Missouri.”

Anati, “Ayi, ndine wa ku Kentucky.” Psyi!

“Sizikumveka mwabwino kwambiri kwa Kentucky,” Ine ndinatero. “Koma, mulimonse,” Ine ndinati, “ngati inu . . . ndi momwe inu mukuganizira, inu kazipitirirani.” Ndipo iye anati—iye anati . . . Ine ndinati, “Inu muyenda bwanji popita kwanu?”

¹⁶⁷ Iye anati, “Ine ndipita chodutsa phiri. Ine ndimakhala kumeneko . . . Chabwino, pitani nane.” Munthu wabwino. Anati, “Mupite nane kunyumba ine, mukakhale usiku wonse, M’bale Branham.”

Ine ndinati, “Ine ndikanakonda ndikanatero, m’bale.” Koma, ine ndinati, “Ine ndikukwera kuno ndi amalume anga.” Ndipo iye anati . . . ine ndinati, “Inu mukufuna kukwera?”

Anati, “Ayi, ine ndiyenera kupita pamwamba pa phiri kumtunda uko, kukwera njira iyi, ndi kutsika chigwembe, ndi kukwera,” inu mukudziwa momwe izo zimakhallira kumusi kumeneko.

Ndipo ine ndinati, “Chabwino,” Ine ndinati, “inu mukafikako bwanji kumeneko?”

Iye anati, “Ine ndikwera ndi njira pamenepo.”

“Bwanji,” ine ndinati, “inu simukutha ngakhale kuliwona dzanja lanu patsogolo panu.” Ine ndinati, “Kodi inu mukafikako bwanji kumeneko?”

Anati, “Ine ndiri ndi nyali!”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, inu muchita bwanji . . . Kodi inu mumachita chiyani, kuyatsa nyaliyo ndi kumayenda nayo iyo?”

Iye anati, “Inde, bwana.”

Ine ndinati, “Inu mukayatsa nyaliyo, kodi inu mutha kuyikwezera iyo mmwamba monga *chonchi*? Ine ndikufuna ndiwone nyumba yanu.”

Iye anati, “Inu simungathe kuyiwona iyo.”

Ine ndinati, “Ndiye inu mukafikako bwanji kumeneko?”

“Oh,” iye anati, “Ine ndingoyatsa nyaliyi; ndipo pamene ine ndikuyenda, iyo . . . Ine ndizingoyenda pamene kuwala . . .”

Ine ndinati, “Ndi zimenezo basi. Ameni, muzingoyenda mu Kuwala.”

¹⁶⁸ Muzingopitiriza kumayenda! Musayime chiriri, inu simukafika kulikonse. Ngati inu mwapulumutsidwa, muyende

mpaka kukuyeretsedwa. Inu mukuti, “Kodi inu mukafika bwanji kumeneko?” Mungopitiriza kuyenda. “Kodi ubatizo wa Mzimu Woyera umakhala kukatha kuyeretsedwa? Kodi ine ndiwupeza bwanji?” Muzingopitiriza kumayenda mu Kuwala. “Ndi zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwitsa...?” Mungopitiriza kumayenda mu Kuwala. Mukuona? Kazingopitirirani basi! Nthawi iliyonse inu mukaponda sitepe, Kuwalako kudumphira patsogolo panu pang’ono, chifukwa Iye nthawizonse amakhala patsogolo panu. Iye samakankha, Iye amatzogolera. Iye ndiye Kuwala. Oh, ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha izo. Sichoncho inu? Iye ndiye Kuwala, mwa Iye mulibe mdima.

¹⁶⁹ “Iwe umadana nazo ntchito za Anikolai.” Zakhala chiphunzitso. Tsopano tiyeni tiwone zimene Paulo... Tsopano, mpingo wandani... Ndani anawuyambitsa mpingo uwu tsopano? Paulo, Efeso.

¹⁷⁰ Tiyeni tibwerere mmbuyo tsopano ku Machitidwe mutu wa 20, miniti yokha. Mu Machitidwe mutu wa 20, ndipo tiwone chimene Paulo... Kodi inu mukukhulupirira kuti Paulo anali mneneri? Ndithudi, iye anali. Ndithudi, iye anali. Mukukumbukira usiku uja masomphenya pa nyanja yamkuntho, ndi zina zotero? Tsopano, ... ndi zonse za izo. Tsopano mutu wa 20 wa Woyera... ya Exo... Machitidwe, ndipo tiyeni tiyambire tsopano pa—pa ndime ya 27, ndipo mvetserani mwatcheru tsopano pamene ife tikuwerenga. Tsopano, uyu ndi Paulo, mneneri, akuneneratu zomwe zidzachitike.

Pakuti ine sindinaleke kulalikira kwa inu uphungu wonse wa Mulungu.

¹⁷¹ Munthu wodala uja! Oh, ine ndikufuna ndidzaima pamenepo tsiku limenelo ndi kudzawona korona wa wofera ameneyo akuikidwa pa mutu wake. Ngati pali chinthu chomwe ine ndikhoza kulira, ndiye ine ndidzalira. Ine ndidzuzuula, kuti ndimuwone Paulo.

Kumuwona Paulo Woyera, mtumwi wamkulu
 uja,
 Mwinjiro wake ukuwala ndi wowoneka bwino;
 Ndipo ine ndikutsimikiza kuti padzakhala ena
 akufuula
 Pamene ife tonse tikadzafika kumeneko.
 (Sichoncho inu?)

¹⁷² Tsopano:

...Ine sindinaleke kulalikira kwa inu... uphungu wonse wa Mulungu.

¹⁷³ Nkulondola uko? Tsopano, Akhristu, yang’anani mbali iyi; ndikufuna kuti ndikufunsi inu chinachake. Anali ndani amene anawalamulira anthu omwe anali atabatizidwa mwanjira ina kupatula Dzina la Yesu Khristu kuti abwere ndi kudzabatizidwanso? [Osonkhana akuti, “Paulo.”—Mkonzi].

Iye analalikira uphungu wonsewo. Nkulondola uko? Oh? Kodi Paulo ananena chiyani mu . . . Ine ndikukhulupirira munali . . . Ine sindikutsimikiza tsopano kaya ndi Atesalonika mutu wa 1 ndi ndime ya 8. “Ngati ife kapena mngelo wochokera Kumwamba angalalikire uthenga wina uliwonse, ngati mngelo atatsika kuchokera Kumwamba ndi kudzalalikira uthenga wina uliwonse wosiyana ndi uwu” (kuposa kulamulira amuna kuti abatizidwenso mu Dzina la Yesu Khristu, ndi Uthenga umene Paulo analalikira) . . . “Ngati mngelo aliyense wochokera Kumwamba” (osati a . . . osatinso bishopu, kapena kardinolo, kapena woyang’anira wamkulu, kapena m’busa, kapena—kapena chinachake) . . . “Ngati mngelo atsika kuchokera Kumwamba ndi kudzalalikira uthenga wina wosiyana ndi uwu, muloleni iye akhale wotembereredwa.” Uko nkulondola. Nkulondola uko? Zomwe iye ananena, ndi Agalatiya 1:8. Ine ndinangopezeka ndikuganiza za izi. Chabwino, Agalatiya 1:8, ngati inu mukufuna kuti mulembe zimenezo, onani zomwe Paulo ananena.

¹⁷⁴ Tsopano, apa iye akuti . . . Tsopano ya 27, ine ndikukhulupirira ndime ya 27:

Pakuti ine sindinaleke kulalikira kwa inu . . . uphungu wonse wa Mulungu.

¹⁷⁵ Tsopano mvetserani zomwe izi . . . Uwu ndi uneneri:

Samalirani kotero kwa inu nokha, ndi kwa gulu lonse, pa . . . chimene Mzimu Woyera . . . unakupangani inu kukhala oyang’anira, kuti muzidyetsa mpingo wa Mulungu, womwe iye wawugula ndi magazi ake omwe.

¹⁷⁶ Ndani anawugula? Anali magazi a ndani amenewo? Baibulo linati iwo anali Magazi a Mulungu. Mulungu, ndi Magazi Ake omwe. Nkulondola uko?

. . . dyetsani mpingo wa Mulungu, umene iye anawugula ndi magazi ake womwe.

¹⁷⁷ Baibulo linati ife tinapulumsidwa ndi Magazi a Mulungu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Ndithudi, Ilo limatero. Chabwino:

. . . wogulidwa ndi magazi ake omwe.

Pakuti ine ndikudziwa ichi, kuti ndikachoka ine idzalowa mimbulu yolusa pakati panu, yosalekerera gululo.

Komanso za inu eni . . . (Penyani, munthu ameneyo amakhoza kuyang’ana pansu kupyola pamenepo ndipo amachiwona chinthu chimenecho chikubwera.) . . . mwa inu eni adzauka anthu, oyankhula zinthu zokhotakhota, kuti adzapatutse ophunzira awatsate iwo.

178 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Zaka mtsogolo monga iye. . . Kapena gulu la amuna omwe akufuna kupanga bungwe ndi kutenga ku—kupatiulika ndi Mzimu Woyera kutali ndi mpingo, ndi kudzaziyika izo pa mabishopu ndi mapapa ndi ansembe, kuti. . . iwo azikhala oyera, ndipo osonkhana azikhala mwanjira iliyonse—mwanjira yomwe iwo akufunira kukhalira. Ndipo iwo nkumawalipira ansembe ndipo iye aziwapempherera iwo kuti achoke ku gehena, ndi china chirichonse monga choncho. Ndipo ndi Chinikolai! Ndipo Mulungu anati, “Ine ndimadana nazo zimenezo!” Tsopano mvetserani.

“Ndiloleni ine ndiwone, ndipo inu mukuti, ‘Mulungu anati Iye ankadana nazo izo?’”

179 Tsopano tiyeni tiwone ngati Iye anatero:

Koma ichi iwe uli nacho, kuti iwe ukudana nazo ntchito za Anikolai, zomwe Inenso ndikudana nazo.

180 Mulungu amadana ndi bungwe. Nkulondola uko? Tsopano inu mukuwona ndendende zomwe iwo amati achite, inu mukuwona zomwe iwo anadzachita. Tsopano tayang’anani kudutsa mu mpingo ngati iwo sakuchita zimenezo. Iye amadana ndi bungwe!

Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu anena kwa mipingo; . . .

181 Tsopano, *mimbulu* ya Paulo inali itasanduka “Chinikolai.” Iwo anali kuyesetsa kuti apange unsembe monga unsembe wa Ulevi, womwe unali wachirendo ku chiphunzitsa cha Chipangano Chatsopano. Amen! Mawu akuti *Nicko*, mawu Achigriki akuti *Nicko* amatanthauza “kugonjetsa, kulanda.” Kulanda chiyani? Anthu wamba, Mzimu Woyera. Kumuchotsamo mu mpingo Ambuye Yesu wowukitsidwa ndi zizindikiro ndi zodabwitsa pakati pa okhulupirira, ndi kuyikamo amuna ovoterredwa kuti akhale papa, kapena wachithupithupi. . . kardinolo, kapena woyang’anira kumayesetsa kuti achotse Mzimu Woyera kuchoka kwa anthu wamba ndi kuwupereka kwa dongosolo lotchedwa dongosolo loyera la anthu, kuwaika iwo *pa* oyang’anira wamba; osati kumawatcha iwo *azibusu* zomwe zimatanthauza “olishya,” koma *atate*; zomwe Yesu anati, “Musamutchule munthu ‘atate’ padziko lino lapansi.” Mukuwona chinthu choyipa chimenecho? Ndipo kodi ife tinachita chiyani?

182 Oh, ngati ife tingaime. Ine ndikanakonda tikanapanda kukhala ndi mausiku onsewa ataunjikidwa monga chonchi, Ine ndikufuna ndidzatenge mawa usiku pa mutu wa 12 wa Chivumbulutso ndi kudzakuwonetsani inu mkazi wachiwerewere wachikulire uja atakhala pamwamba apo, hule. Ndipo iye. . . chifukwa chomwe iye anali, chifukwa iye anali atachita ziwerewere. . . ndi Mulungu, ndipo amadzitcha yekha wamasiyey, ndiponso iye anali mayi wa achiwerewere.

Nkulondola uko? Tsopano, ife tikudziwa kuti uyo anali Roma, chifukwa iye anali atakhala pa mapiri seveni, ndipo chirichonse chimodzimodzi basi, mwamuna mwa iye ndipo ndi nambala ya chirombo, ndi zina zotero. Ife tonse tikudziwa zimenezo kuchokera ku ziphunzitso zapitazo, yemwe iye anali. Koma chinthu chomvetsa chisoni chake, iye anali mayi wa timahule. Ichi ndi chiyambi cha iye pomwe pano, kuyambira mu Roma ngati gulu la Akhristu, otchedwa Akhristu.

¹⁸³ Tamvetserani! Mulungu andithandize ine kuti ndichite zenizeni! Gulu la Akhristu mu mpingo ngati uwu. Iwo anakhala ofunda, ndi osayanjanitsika, ndipo anachokapo, ndipo anakadzikhazikitsira okha bungwe. Ndiyeno anzilumikiza zimenezo, mu M'badwo wa Mdima, ndi boma. Ndipo boma ndi mpingo zinadzakhala chimodzi chiyani? Mpingo wa Chikhristu, "Mpingo Woyera wa Katolika" iwo unkatchedwa, (Mawu akuti *Katolika* ndi, mawuwo amathanthauza, "wapadziko lonse"), "mpingo waukulu wa Chikhristu wapadziko lonse lapansi." Ndipo ankawatcha anthu omwe ankayankhula mmalirime, ndi kufuula, ndi kuchiritsa odwala, ndi zina zotero, "ampatuko." Ndipo potsiriza pake anazipanga izo kukhala zovuta kwambiri mpaka aliyense yemwe anapezeka akupembedza mwanjira imeneyo, anaponyedwa mu dzenje la mikango, ngati savomereza Chikatolika. Izo zimachitika kwa zaka mahandiredi onse awa kumbuyo uko za kuzunzika kumeneko. Koma Mpingo umenewo sunafe konse. Inu simungathe kuwupha Iwo. Mulungu anati Iwo udzakhala moyo mpaka kumapeto ndiyeno Iye adzawupatsa Iwo korona wa Moyo. Kubwera kudutsa mu mibadwo imeneyo ya kuzunzika.

¹⁸⁴ Ndiye potsatira kunadzabwera Martin Luther kuti adzapitirize m'badwo ndipo iye anadzawugwedeza mpingo pansu pa kulungamitsidwa. Chinachitika ndi chiyani pamene Luther anafa? Iwo anawupanga iwo bungwe, anawupanga iwo mpingo wa Chilutera; iwo anapeza chiphunzitso. Pamene iwo anawupanga bungwe, kodi iwo anachita chiyani? Anawupatsa iwo kubadwa kubwerera mu Chiroma kachiwiri. Kulondola ndendende.

¹⁸⁵ Zitatero Mzimu Woyera unadzachoka mwa iwo ndipo Wesley anaziwona Izo. Ndipo Wesley, ndi Whitfield, ndi George Whitfield, ndi ena ambiri a iwo, ndi—ndi Asbury, ndi ambiri a iwo anali azitsitsimutso zopambana. Iwo analipulumutsa dziko mu tsiku limenero. Iwo anali ndi chitsitsimutso mu M'badwo wa Filadefiya umenewo umene unapulumutsa England, ndi United States nayenso. Iwo anali ndi misonkhano kumene iwo anathamangitsidwira panja ndipo anatchedwa "oyera odzigudubuza." Inu a Methodisti munali, munachita zimenezo; iwo anagwera pa dothi pansu pa mphamvu ya Mulungu, ndipo ankaponyera madzi pankhope pawo ndi kumawakupiza iwo. Uko kulondola. Ndipo iwo anagwedezeke mwamphamvu

pansi pake, mpaka iwo anafika...mpaka iwo anati “iwo anali ndi kunjenjemera.” Panali anthu amene amanjenjemera ndi kugwedezeka pansu pa mphamvu ya Mzimu Woyera. Ndi imeneyo mbiriyakale ya Methodisti. Kuchokera pamenepo kunadzabwera ma Quakers ndi ena otero; apa tsopano anali atazipanga izo bungwe.

¹⁸⁶ Iwo anapanga Methodisti *iyi*, Methodisti Yachimidzi, ndi mtundu *uwu* wa Methodisti, ndi mtundu *uwo* wa Methodisti, mpaka izo zinafika potsika kwambiri mpaka anthu Achimethodisti ankafuna kuchotsa “Magazi” kuchokera mmabuku awo a nyimbo.

¹⁸⁷ Apa usiku wina, pa purogaramu ya televizioni (Amayi anga anandiitana ine.) iwo anali ndi m’busa wa Methodisti, komwe kuno ku Indiana, akuphunzitsa gwedemula mu mpingo. Anati, “Ndi zomvetsa chisoni kuti ife talephera kuwona luso lokongolali lomwe likulowa mu mpingo.”

¹⁸⁸ Ameneyo ndi mdierekezi mwa mneneri wabodza! Kulondola! Sindikufuna kuti ndivulaze kumverera kwano koma, m’bale, ndicho Choonadi cha Mulungu. Ine kulibwino ndikukwiyitseni pang’ono mwanjira iyi ndi kukupangitsani inu kuphunzira Lemba, mwinamwake kuyanjana ndi Mulungu, kuposa kudzatayika pamapeto. Inu mukhoza kusandikonda ine tsopano, koma tsiku lina inu mudzaika dzanja lanu mondikumbatira ine, nkuti, “M’bale Branham, icho ndi Choonadi.” Ndi izi apa pomwepa, ndipo kupita kwawo mu zimenezo. Ndi kumene iwo... Izo ziri pamenepo. Baibulo linati iwo akanadzachita zimenezo.

¹⁸⁹ Ndiye kuchokera kwa Wesile, ngati Wesile anachita zimenezo, ndiye motsatira kunadza Achipentekoste. Ndipo iwo anapeza kubwezeretsa kwa mphatso, anayamba kuyankhula ndi malirime, ubatizo wa Mzimu Woyera.

¹⁹⁰ Chimodzimodzi monga mbewu ya chimanga imatuluka mnthaka. Chinthu choyamba, iyo imavunda. Imabweretsa masamba angapo. Ndiye izo... Inu muli ndi munda wa chimanga, inu mukuganiza. Tsamba limenelo limakula ndipo limadzapanga ngayaye. Choyamba ichi, chinali Chilutera. Ngayaye, chinali chiyani icho? Methodist; mungu, chikondi chapaabale, uvangeri, mungu kumatulukapo kumapita kwa enawo.

¹⁹¹ Bwanji, ngakhale chirengedwe chimadzinenera mibadwo ya mpingo iyi. Amethodisti akutuluka mu chisokonezo... kapena, ine ndikutanthauza, Achilutera akutuluka mu chisokonezo. Amethodisti akugwedezeka chikondi chawo chapaabale, ndi tsiku la uvangeri, ndi—ndi tsiku la—la umishonare. Tsiku lalikulu umishonale kwambiri lomwe dziko silinalidziwepo linali nthawi ya Amethodisti. Ndiko kulondola. Akugwedezapo mungu wake.

192 Nchiyani chinachitika kunja kumeneko? Kuchokera mu mungu uja munabwera mbewu ya chimanga, Achipentekoste. Mbewu, chimodzimidzi monga chinthu chomwecho chinadzalowamo. Osati tsamba, osati ngayaye, koma mbewu. Ndipo tsopano a—Achipentekoste ali ndi chuku pa mbewu zonsezo, mpaka iyo...inu simungaiwone nkomwe mbewuyo. Yakwana nthawi yoyeretsa izo! Ameni! Kodi iwo anachita chiyani? Anachita chinthu chomwe chomwecho chimene Amethodisti anachita. Mmodzi anawapanga iwo kukhala gulu, anati, “Ndife a Assemblies of God.” Mmodzi winayo, “Ndife a Pentecostal Holiness.” Mmodzi wina, “Ndife Aumodzi.” “Ndife a Uwiri.” Ndipo—ndipo pali zochuluka za *izi*, ndi zochuluka za izo. Mai! Wokwera ngamila ya nthumbira imodzi kunsana, nthumbira ziwiri, nthumbira zitatu, chirichonse. Oh, alipo sikisite, kapena sarte, kapena mabungwe forte osiyanasiyana a iwo.

193 Kodi iwo anachita chiyani? Anaziponya izo kubwerera mu Chiroma kachiwiri, amabatizidwa mu ubatizo wa Tchalitchi cha Roma Katolika. Ine ndikufunsa wa Chipentekoste aliyense kuti andiwonetse ine kumene aliyense mu Baibulo anabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ine ndikufunsa bishopu aliyense, kardinolo, mphunzitsi aliyense, kuti andisonyeze ine kumene izo zinayamba zachitikapo, anayamba achitipo kunja kwa mpingo wa Katolika. Ndipo Lutera anabweretsa izo limodzi ndi iye, iye anabweretsa katekisima ndi china chirichonse kuchokera mmenemo. Amethodisti anapitirira nazo. Achipentekoste, inu muyenera kuchita manyazi! Konzani! Bwererani ku Mawu! Mulape apo ayi Mulungu akuchotserani choyikapo nyalicho kwa inu, Kuwala komwe inu muli nako. Ameni! Chabwino.

194 Kuwuchotsapo Mzimu Woyera ngati Mtsogoleri, ndi kuwapatsa iwo dongosolo loyera la amuna, ndi kuwuyika iwo pa anthu wamba. Ndipo musamawatchule iwo “abusa, olisha,” (Ife timayenera kumatchedwa *azibusa*, “olisha,” mawu akuti *m’busa* amatanthauza.) koma “bambo, kardinolo, bishopu wamkulu, kapena woyang’anira wamkulu.” Woonawo amadana nacho chinthu ichi! Ndipo Mulungu anavomereza izo mmalo mwawo, ndipo anati, “Ine ndimadana nazo izo, nanenso!” Chifukwa Iye akuyenera kukhala woyang’anira wamkulu, bishopu wamkulu, komanso papa. Iye amagwira ntchito ndi munthu aliyense payekha; osati bungwe, koma munthu.

195 Tsopano, modabwitsa...Mvetserani, pamene ife tikufika kotseka. Ife tangotsala ndi ndime imodzi ina.

196 Apa ife tiri ndi chiphunzitsi cha chiyambi cha Chikatolika, utumwi wolowezana. Ndi angati amadziwa zimenezo? Mtumwi. Tsopano Akatolika amanena kuti “Papa lero ndi wolowa mmalo mwa Petro, utumwi wolowezana.” Kulibeko chinthu choterocho. Kodi chilakolako chanu chachithupithupi, chogonana chiri

bwanji. . . Zinatheka bwanji kuti Esau ndi Yakobo awiri onsewo abadwe ndi bambo woyera ndi mayi woyera, ndipo mmodzi wa iwo ndi Mkhristu ndipo winayo ndi mdierekezi? Uh-hum. Izo zingatheke bwanji? Chifukwa tchimo ndi tchimo, ndipo kugonana ndi kugonana, koma Mulungu ndiye amapereka Kubadwa.

¹⁹⁷ Mulungu amatisankha ife kuchokera ku maziko a dziko. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Dikirani mpaka ife tidzafike powerenga azambiriyakale awa, ndipo mudzawone momwe Ireniasi. . . momwe iye amaperekeramamando kwa Mulungu chifukwa chomusankha iye asanaikidwe maziko a dziko; momwe kuti Martin Woyera uyo ndi onse awo, akumamupatsa Iye matamando; Mulungu, matamando. Anati, “Chifukwa. . .” Ndipo akuyankhula za Iye, kuti, “Iye anasankhidwa asanaikidwe maziko a dziko lapansi.” Ndiro Lemba. Abale amenewo anali pa mzere ndi Mulungu. Koma mpingo wakale wakuda uwu unabwera kudutsa mu zaka fifitini handiredi za Mibadwo ya Mdima, anachichititsa mwaye chinthu chonsecho ngati nyali ikufuka, kuchititsa khungu Kuwala. “Koma kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo,” Ambuyeye anatero.

¹⁹⁸ Kulowezana kwautumwi, mmodzi pambuyo pa mzake; papa mmodzi, ndipo iwe uyenera kukhala mu mzere wa mapapa iwe usanakhale papa. Oh, mai, mai! Ndizo zamkutu. A—anthu wamba. . . Osati oyera ndi olungama, koma. . . lolani. . . lolani—ansembe awapempherere iwo ndi kuwatulutsa iwo ku machimo awo, kuwakhulukira machimo awo, kulipira ndalama kuti alape.

¹⁹⁹ Achiprotostanti nawonso amachita zomwezo! Iwo amayesetsa kuti akhale. . . amawasisita abusa awo ku nsana ndi kumakhala monga dziko lonse lapansi. Ndipo iye sadziwa zochulukira za Mulungu kuposa momwe iye amadziwira. . . amawalola iwo kuti azikhala mu mpingo wake ndi kumawatcha iwo mamembala a mpingo wake, ndi kuwalola iwo kuti akhale mmenemo ndi kumanena kwa iwo kuti iwo ndi opulumutsidwa. Momwe iwo ati adzakhumudwitsidwire pa tsiku limenero ngati iwo sanabadwe mwatsopano! Popanda Mzimu Woyera iwe watayika. Palibe munthu anganene, “Yesu ndi Khristu,” kokha mwa Mzimu Woyera.

²⁰⁰ Mpingo woona ku Efeso sunanyengedwe ndi malankhulidwe opukutidwawa, aluntha. Iye. . . Iwo ankadana nazo izo. Iwo sananyengedwe, iwo akudziwa; Mpingo woona sunali.

²⁰¹ Vumbulutso labodza lomwe anthu awa anali nalo, lotchedwa Chinikolai, lomwe silimagwirizana ndi Mawu a Mulungu. Ndiuzeni ine komwe inu munawonako “wansembe ali pa kulapa” zikuphunzitsidwa mu Baibulo apa. Kodi inu munawonako kuti “kukonkha” kukuphunzitsidwa mu Baibulo apa kuti ndi chikhulukiro cha tchimo? Ndi pati pamene

inu mumawonapo aliyense akubatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” ku chikhululukiro cha tchimo lanu? Kodi inu munawonapo kuti izi, “Zopereka dzanja lamanja la chiyanjano, ndi kulemba dzina lawo pa bukhu la mpingo” mmenemo? Kodi inu mumaziwonapo pati zinthu zonsezi? Icho ndi chiyani? Ndi unsembe kapena a—m’busa yemwe sali limodzi ndi Mawu, ndipo iwo ndi Achinikolai, ndipo Mulungu anati, “Ine ndimadana nawo!” Bwererani ku Mawu. Oh, ndizo. . . Ine ndikudziwa kuti zimenezo ndi zolimba, abale, koma ine—ine—ine ndiribe choyankhira; kwa Yesu, kukangana ndi Iye.

²⁰² Vumbulutso labodza, losagwirizana ndi Mawu, koma, anawatcha iwo “abodza, atumwi abodza, aneneri abodza.” Koma Mpingo woona unagwiritsitsa ku chiphunzitsa choyambirira cha Paulo Woyera ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi zizindikiro zikutsatirapo ndi kutsimikizira Mawu amene Paulo ankaphunzitsa. Ameni! Ndiwonetseni ine pamene Mulungu anatsimikizirapo konse mawu a kukonkha. Ndiwonetseni ine pamene Mulungu adzatsimikizire konse, ndi kubweretsa kuyankhula mmalirime ndi zinthu zazikulu, pongogwirana chanza ndi abusa kwinakwake ndi kulemba dzina lanu pa bukhu; ndipo nkumatafunabe, kusuta, kumamwa, kumanena mabodza, maphwando amakadi, kusangalala pang’ono, kupita. . . Oh, chifundo! Ameneyo ndi mneneri wachithupithupi, wabodza, mzanga. Inde, bwana.

²⁰³ Njira ya Mulungu ndi yachiyero. Mulole ichi chidziwike kwa membala aliyense pano wa Thupi la Khristu: mpaka inu mutakhala moyo wachiyero, Mulungu amakana nsembe yanu. Nsembeyo iyenera kuperekedwa ndi manja oyera. Ndizo. . .? . . . kulondola. Wansembe wamkulu asanalowe nkomwe kuti adzapereke nsembe, iye amayenera kukhala woyera, ndi wodzipereka, ndi wodzozedwa, ndipo atanunkhiritsidwa, ndi chirichonse, asanayende nkomwe mu kukhalapo kwa Mulungu kuti akapereke nsembe. Nkulondola uko? Ndiye iwe ungate bwanji kupita kunja kuno ndi kukanama, ndi kukaba, ndi kukangana, ndi kumanyana ndi anansi ako, ndi china chirichonse, ndi kumapitirira momwe inu mumachitira, ndiyeno nkubwera mmenemo ndi kudzati, “O Ambuye Mulungu! Matamando kwa Yesu! Aleluya!”?

²⁰⁴ Anthu amati, “Ine ndikuwawona iwo akuyankhula mmalirime.” Zimenezo sizikutanthauzabe kuti ali ndi Mzimu Woyera. “Ine ndimawamva iwo akufuula.” Zimenezo sizimatanthauzabe kuti iwo ali ndi Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi moyo.

²⁰⁵ Baibulo linati, “Mvula imagwa pa nthaka nthawi zambiri, kuti ikakonzekeretse izo, ndi kuziveka izo chomwe izo zinakonzedwerako,” (Ahebri 6) “koma minga ndi nthula zomwe zatsala pang’ono kukanidwa, zomwe matsiriziro ake ndi kuwotchedwa.”

206 “Dzuwa limawala pa olungama ndi osalungama. Mvula imagwera pa olungama ndi osalungama.” Mvula imabwera kudzapanga mbewu ya tirigu (ife tidzitcha izo), ndi udzu uliwonse womwe uli mmunda. Ngati tirigu akumva ludzu, ndiye kuti udzu uli ndi ludzu. Ndipo mvula yomweyo yomwe imathirira tirigu, imathirira—imathirira udzu nawonso. Tirigu wamng’ono wakale amakweza mutu wake ndikufuula, “Ambuye alemekezeke! Aleluya! Aleluya! Ndine wokondwa kuti ndalandira mvula iyi!” Udzu waung’ono udzafuula, “Ulemelero kwa Mulungu! Mulungu alemekezeke! Aleluya! Ndine wokondwa kuti ndalandira iyo.”

207 “Koma ndi zipatso zawo inu mudzawazindikira iwo.” Uko nkulondola. “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.”

208 Ndime ya 7, ndiyeno ife tikutseka, uwu ndi wotsiriza wa m’badwo wa mpingo. Tsopano ife tichedwa ndi pafupifupi maminiti faivi, kapena teni, miniti yokha.

*Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene
Mzimu akunena kwa mipingo; Kwa iye amene agonjetsa
Ine ndidzampatsa kuti adzadye za mtengo wa moyo,
umene uli pakati pa paradaiso wa Mulungu.*

209 Tsopano tayang’anani, abwenzi, umu ndi mmene inu mumagonjetsera. Choyamba inu mumayenera kugonjetsa, kenako inu mukhoza kudya chipatsocho. Ndi wogonjetsa. Inu mukukumbukira usiku wina, kuphunzitsa kwathu usiku watha? Yohane amayenera kulowa mu Mzimu iye asanawone kalikonse. Ndipo inu mungakhale bwanji, nkumati, “Ngati iye si wa Baptisti, ine sindipita kuti ndikamumvetsere iye?” “Ngati iye si wa Presbateria, ine sindipita kuti ndikamumvetsere iye.” “Ngati iye saphunzitsa ndendende zomwe mpingo wanga umaphunzitsa, ine. . .” Inu—inu—inu simugonjetsa, inu simunalowebe mu Mzimu apabe. Inu nonse mwatuluka mu dongosolo.

210 Mulowe mu Mzimu, ndikuti, “Ambuye Yesu, ine ndimakukondani Inu, tsopano ndiululireni ine chirichonse chimene Inu mukuwona kuti ndi choyenera, mungochibweretsa icho kwa ine.” Zikatero ndinu—zikatero zikukuyenderani bwino. Ndiko kulondola.

211 Zindikirani, katatu Baibulo likuyankhula za—za Mtengo wa Moyo mu Genesis, katatu mu Bukhu la Chivumbulutso. Tsiku lina ife tinali nazo izo. Mukukumbukira? Lamlungu, dzulo. Chokhacho. . . Mdierekezi amadana ndi chidutswa chirichonse cha Lemba chomwe chiripo, koma iye amadana, moyipitsitsa, Genesis ndi Chivumbulutso. Iye amamenyana ndi Genesis chifukwa cha kuvomerezeka kwake, chifukwa iye amafuna kuti awapangitse anthu akhulupirire kuti Izo sizinali chomwecho; “Genesis sanabwere mwanjira imene Mulungu ananenera kuti iwo anachitira, panali china chakenso chomwe chinayambitsa

chirengedwe ichi ndi chinthu.” Ndiye iye amamenyana nalo Ilo mwanjira imeneyo. Ndipo iye amawatengera anthu kutali ndi Chivumbulutso chifukwa Ilo limaulula: Yesu pokhala Mulungu, ndipo iye pokhala mdierekezi (ndipo iye wawonongedwa), ndipo ulemelero wa Mpingo woyeretsedwa wopita kwawo kwa Mulungu, ndi chiwonongeko cha mneneri wonyenga, ndi onse amene amanama ndikuchita chirichonse adzaponyedwa mu nyanja yamoto. Ndi zosadabwitsa kuti iye amawasunga iwo kutali ndi Iwo. Koma, kumbukirani, malo onsewa amalankhula za Mtengo wa Moyo mu Paradaiso.

212 Tsopano tiyeni titenge izi miniti yokha, ndipo tsopano “Mtengo.” Yohane Woyera mutu wa 6, ngati inu mukufuna kulemba izo, Yesu anati, “Ine ndine mka—mka—Mkate wa Moyo.” Tsopano, kumbukirani.

213 Tsopano ife tigwiritsa ntchito mizati iwiri iyi ngati chophiphiritsira apa. Chotero, basi tisanatseke, tsopano. Tsopano, kudzanja langa lamanja kuli mtengo mmunda wotchedwa Mtengo wa “Moyo,” kudzanja langa lamanzere kuli mtengo mmunda womwe umatchedwa mtengo wa “chidziwitso.” Ndi angati akudziwa kuti Baibulo limanena kuti pali Mtengo wa Moyo ndi mtengo wa chidziwitso? Tsopano, munthu ankayenera kuti azikhala moyo ndi Mtengo wa Moyo uwu, osati kuti aziwukhudza mtengo wa chidziwitso. Nkulondola uko? Ndipo nthawi yoyamba yomwe iye anaugwira iwo, iye anadzilekanitsa kwa Mlengi wake. Iye anataya chake—chiyanjano chake ndi Mulungu pamene iye anatenga kuluma kwake koyamba kwa chidziwitso. Tsopano, talingalirani molimba tsopano. Ndipo inu mukulemba zolemba zanu, ine ndikupatsani nthawi kuti muthe kuzipeza izo, chifukwa ine sindikufuna kuti muphonye izi.

214 Yesu, mu Yohane Woyera 6. Iwo anali kumwa kuchokera pa kasupe, ndi kumaponyera mmwamba manja awo ndi kumachita mnyozo pamenepo, kuti, makolo awo ankamwa kuchokera ku Thanthwe lauzimu, ndi zina zotero. Iye anati, “Ndine Thanthwe limenelo lomwe linali mchipululu.”

215 Ndipo iwo anati, “Apa inu mukunena kuti ‘munalipo asanakhalepo Abrahamu,’ ndipo ndinu bambo wosadutsa zaka fifite zakubadwa. Ndipo inu mukunena kuti inu ‘munamuwona Abrahamu’? Ife tazidziwa zimenezo tsopano, kuti, ndinu wamisala, ndinu mdierekezi.” Mukuona?

216 Iye anati, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.” INE NDINE anali mu chitsamba ndi Mose; chitsamba choyaka, INE NDINE. “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE”; osati “Ine ndinali.”

217 Tsopano, anthu inu amene mumati masiku a zozizwitsa anapita, inu muyenera kulipanga Lemba limenelo kuti liziti, “Ine ndinali wamkulu Ine ndinali.” Mukuona?

218 Osati “Ine ndinali,” kapena “Ine ndidzakhala”; “INE NDINE,” ndizo nthawi zonse. Iye ndi Wamuyaya. Mawu akuti “INE NDINE” ndi Wamuyaya, m’badwo wawo wonse, nthawi zonse, mu zoyikapo nyali seveni zagolide zonse, mpingo uliwonse, malo aliwonse, mtima uliwonse. “INE NDINE,” (osati “Ine ndinali” kapena “Ine ndidzakhala”) “Ine ndiri pakadali pano monga ine ndinali nthawizonse.” Mukuona? “Nthawizonse, INE NDINE.”

219 Iwo anati, “Makolo athu...Ife sitikukudziwa iwe. Ife tikudziwa kuti ndiwe mdierekezi.” Anati, “Makolo athu ankadya mana mchikululu kwa zaka forte.”

220 Ndipo Yesu anati, “Ndipo iwo aliynense wa iwo anafa.” Kulondola uko? “Iwo onse anafa. Koma ine...” Oh! “Ine ndine Mkate wa Moyo wochokera kwa Mulungu Kumwamba. Ngati... Mkate wa Moyo. Ngati munthu adya Mkate uwu sadzafa konse.”

221 “Kodi munthu uyu apereka thupi lake, kuti tidye?” iwo anati, “Tsopano iye wachita misala, zoonadi ndithu.”

222 Mkate wa Moyo unali wochokera ku Mtengo wa Moyo, kumene iwo anali kudya, kuchokera mmunda wa Edeni. Iye anali Mtengo wa Moyo. Tsopano, ngati Mtengo wa Moyo unali Munthu, ndiye mtengo wa chidziwitso unali munthu. Tsopano nenani kuti serpenti analibe mbewu! Ngati Moyo umabwera ndi Mwamuna, imfa imabwera ndi mkazi. Chabwino, iye anali mtengo wa imfa.

223 Mwamsanga pamene—pamene mmodzi uyu anamuyipitsa iye, chimene iye anachita (serpenti), iye anati, “Serpenti wandinyenga ine.” Uko nkulondola. Osati njoka; iye anali wochenjera kwambiri pa zinyama zonse, iye anali pakati pa chimpanzi ndi munthu. Mbewu ya nyama siingalumikizane ndi mkazi, siingachite zimenezo; koma munthu uyu anali, iye anali cholumikizira chotsatira kwa icho. Ndipo Mulungu anamuyikira themberero loterolo pa iye Iye anamubwezeranso iye kuti abwerere pamimba pake, ndi wopanda miyendo, ndipo anachotsa fupa lililonse mwa iye ndipo analisintha ilo kuchokera ku chirichonse chonga munthu. Sayansi imayetsa kuti ikachikumbe icho mmunda. Zimenezo zinabisika mu zinsinsi za Mulungu, mkati mwa Paradaiso wa Mulungu. Ndi limenelo vumbulutso lanu.

224 Iye anabala mwana wake wamwamuna woyamba yemwe anali Kaini (Nkulondola uko?), mwana wa Satana, mwana wa Satana. Ngati iwo sanatero, kodi chimenecho—kodi woipa uja anachokera kuti? Anachokera mwa Adamu yemwe anali mwana wa Mulungu? Anachokera kwa mdierekezi, abambo ake. Ndipo anamupha; wakupha woyamba anali mdierekezi, mwana wa mdierekezi.

225 Tapenyani zomwe zinadzachitika zitatha zimenezo, penyani mzere wa Kaini. Kudutsa mpaka mmusi kupyola m’badwo

uwo womwe unatsatira, pambuyo pa Kaini, mmodzi aliyense anali wasayansi ndi amuna otchuka. Kawerengeni Baibulo. Iwo anamanga manyumba, iwo amagwiritsa ntchito zitsulo, ndipo iwo anali asayansi. Koma aliyense yemwe anabwera kuchokera kwa Seti, (Chimene Abele anafa, choyimira cha Yesu, anafa; ndipo Abele anafa, ndipo Seti anatenga malo ake: imfa, kuyikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro). . . kuchokera kwa iye kunadzabwera alimi odzichepetsa, olisha nkghosa anabwera chotsika kudutsa zimenezo.

²²⁶ Tsopano Yesu anati, “Makolo anu anadya mana mchipululu ndipo iwo onse anafa. Koma Ine ndine Mkate wa Moyo umenewo,” (Mkate wa Moyo wake uti? Kuchokera mu Edeni!) “kuti munthu akadya Mkate uwu asafe konse.” Tsopano, Mulungu anaika Mngelo kuzungulira Mtengo wa Moyo umenewo, kuti aziwutetezera iwo kuti pasakhale aliyense woti awukhudze iwo, pokhapokha iwo adye Mtengo umenewo ndi kukhala moyo kwanthawizonse. Nkulondola uko?

²²⁷ Chifukwa, iwo amayenera azipitirira pa mtengo uwu ndi kumafa. Nkulondola uko? Chifukwa, nthawi yonse imene iwo amadya za iwo, iwo amafa. Ndipo motsimikiza basi monga momwe inu mumafa chifukwa mwadya za mtengo wa chidziwitso. . . Tsopano, tiyeni tiyang'ane pa mtengo wa chidziwitso umenewo tsopano. Taonani zimene iwo unachita. Tsopano tiyeni tiwone zimene iwo wachita. Chinthu choyambirira, tiyeni tiwone, izo. . . Chabwino, tiyeni tiwone chimodzi chomwe iwo. . . iwo unapanga wonga wa mfuti. Iwo umapha anzathu. Uko nkulondola, kuphana wina ndi mzake ndi wonga wa mfuti, kuchokera pamtengo wa chidziwitso. Chotsatira chomwe ife tapanga, mai, tiyeni tiwone, ife—ife tinapanga galimoto, kuchokera ku mtengo wa chidziwitso umenewo. Iyo imapha anthu kuposa momwe onga wa mfuti umachitira. Oh, eya! Tsopano, ife tiri ndi bomba la haidrojeni. Mulungu samawononga kalikonse, munthu amadziwononga yekha ndi chidziwitso chake.

²²⁸ Koma onse amene ali a Mulungu, Mulungu adzawawukitsanso iwo; Mulungu samataya chirichonse. Yesu ananena chomwecho, ndiko kulondola, “Iye amene adya Mkate uwu ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Ine ndidzamuukitsa iye kachiwiri tsiku lomaliza.” Ndiri lonjezo Lake. Tsopano, Mulungu. . .

²²⁹ Iwo ali patsogolo kwambiri, akudya pa mtengo wa chidziwitso ndipo akumafa. Koma mwamsanga iwo akanangofika ku Mtengo uwu, iwo akanakhala ndi moyo kwanthawizonse.

²³⁰ Chotero tsopano mmalo mwa Mngelo kunjia uko akuwaletsa iwo kufika ku Mtengo uwu, ali kunjia uko akuwalondolera iwo kuti apite *ku* Mtengo uwu; angelo a mipingo, mipingo isanu ndi iwiri, kuwabwezera iwo ku Dzina la Yesu Khristu

yemwe ali Mtengo wa Moyo womwe ukuyima mu Paradaiso wa Mulungu. Psyi! Mai! Ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa zimenezo. Mtengo wa Moyo ukuyima mu Paradaiso wa Mulungu kuti inu mukamudye Iye ndikukhala mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu ndi kukhala ndi moyo kwanthawizonse. “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

²³¹ M'bale, mlongo, tsopano ine ndiri...Ine...Ndithudi, ndatero...Ine—ine ndakudulani inu, ndakupwetekani inu. Ine—ine sindimatanthauza kuti ndichite izo chomwecho. Mukuona? Mulungu akudziwa zimenezo, koma ine ndiyenera kuchita izo mwanjira iyi kuti ndikuloleni inu muwone kumene ife tiri. Ine sindikukhulupirira kuti ife tatsala ndi nthawi yambiri yoti tizikhalapo. Ine sindikuyesera kuti ndikupangitseni inu kuti sindinu akhristu chifukwa ndinu a bungwe. Si zimenezo ayi. Anthuwo amapezeka mu zochitika zosawakhudza. Iwo samadziwa zoti achite; zonse zimene makolo awo akhala akuchita nthawi zonse ndi kupita kukajowina tchalitchi ndi zinthu.

²³² Koma, m'bale, chinthu chimodzi ife tisananyamuke, ndiroleni ine ndipange chobwereza chimodzi ichi. Mneneri anati...Kodi inu mumakhulupirira aneneri? Baibulo linati tiziwamvetsera iwo. Mneneri anati, “Idzafika nthawi yomwe sipadzakhalanso usana kapena usiku, koma lidzakhala ngati tsiku lachimbuuzi. Koma mu nthawi yakumadzulo, dzuwa lisanalowe kumene, kudzakhala Kuwala.” Nkulondola uko?

²³³ Tsopano taonani zomwe ife takhala nazo. Tsopano, tiyeni tingoyang'ana. Dzuwa limapanga bwanji...Dzuwa limatulukira kuti, mwa malo? Kummawa. Nkulondola uko? Ilo limakalowa kumadzulo. Ine ndikanakonda ndikanakhala...Ine nditenga mapu mawa usiku ndi kudzakuwonetsani inu. Pamene Mzimu Woyera unagwa mu Yerusalemu, Iwo unapanga chilembo changwiro cha eyiti, njira Yake. Iwo ukupita molunjika kumene kudutsa mu Ireland, kubwerera nkudzazungulira, kudzawoloka, ndi kudzabwera ku Gombe la Kumadzulo, ndi kudzagweranso komweko; chilembo changwiro cha eyiti komwe Uthenga unapita. Tsopano, chitukuko chayenda limodzi ndi dzuwa. Ndi angati akudziwa zimenezo? Inu mwaphunzitsidwa zimenezo ndipo mukuzidziwa zimenezo. Chitukuko chakale kwambiri chimene ife tiri nacho ndi China, ndiyeno kuchokera kumeneko icho chinadzawoloka mpaka kummawa. Ndipo pamene Mzimu Woyera, osati d-z-u-w-a, koma M-w-a-n-a. . .

²³⁴ Pamene dzuwa, d-z-u-w-a, liyamba kuwala kudzera mu chifunga ndi nkhungu za usiku, ziribe kanthu komwe mbewu ili, iyo idzakhala moyo; chifukwa moyo wa zomera wonse umakhala moyo ndi dzuwa. Ife tikudziwa zimenezo.

Inu mukhoza kutsanulira konkire pa chidutswa cha udzu, ndipo chirimwe chotsatira, udzu wonenepa kwambiri uli kuti? Kumapeto kwenikweni kwa konkire. Chifukwa chiyani? Ndi moyo umenewo pansi pamenepo, inu simungakhoze kuwubisa moyo weniweni. Moyo wawung'ono umenewo, mwamsanga iwo ukangodziwa kuti dzuwa likusamba modutsa pamenepo, iwo umakwawa mozinyolola kwa theka la mdadada wa mu mzinda, kumayenda mozungulira pansi pa konkire imeneyo mpaka iwo umatha kukweza mutu wake mmwamba mumlengalenga ndi kumapita ukulemekeza Mulungu.

²³⁵ Inu simungakhoze kuwubisa Moyo. Ndiko kulondola, MOYO. Pamene inu mwabadwa mwatsopano inu simungakhoze kuwubisa Iwo. Chinachake chimayenera kulira pamene iwe wapeza Moyo.

²³⁶ Tsopano, zinthu zonse zomwe zafa tsopano, ndi mbe—mbewu zazing'ono zimaphulika nkutseguka, zamkati zimatulukapo, ndipo ndi yakufa, koma moyo ulipo mmenemo. Tsopano, pamene dzuwa liyamba kuwala mu chirimwe, malwa ang'onoang'ono amatuluka, ndipo chirichonse chimakweza mutu wake mmwamba aponso (kutuluka kuchokera pansi pa zibanthu, kutuluka kuchokera pansi pa zipika, kuchokera pansi pa miyala), izo zimaukanso, ndi kukhalanso moyo kachiwiri. Nkulondola uko? Chifukwa d-z-u-w-a likuwala.

²³⁷ Tsopano, tsiku lina M-w-a-n-a adzawala, yemwe ali Woyambitsa Moyo Wamuyaya, ndipo chirichonse chomwe chameretsedwera kwa Iye kwa Moyo Wamuyaya, Iye anati, “Ine ndidzachiukitsanso icho mu tsiku lomaliza.” Inu mukuwona zimene ine ndikutanthauza? Moyo Wamuyaya udzaukitsidwa mu masiku otsiriza. Ngati iwo adzakukwirirani inu mu nyanja, kapena iwo atenthe thupi lanu ndi kuliponyera ilo ku mphepo zinai za dziko lapansi, Mulungu adzawuwukitsa iwo mu tsiku lotsiriza. Ngati inu muyenera kudzaza mimba ya mkango wanjala, kapena—kapena kupita mmaenje amoto omwe angatenge zonse ma—ma—maphulusa sikisitini ndi kuwala kwa dziko ndipo chirichonse kuzichotsa mwa inu, Mulungu adzaziwukitsa izo. “Tsitsi kumene la mmutu mwanu limawerengedwa.” Ameni! Mulungu adzaliwukitsa ilo!

²³⁸ Tsopano, taonani apa. Tsopano, ngati munthu aliyense amafa mwa mkazi, ndiye kuti munthu aliyense amakhala moyo mwa Mwamuna. Kutengako za mkazi mu moyo wa mtundu umenewo, inu mukudziwa kuti inu mudzafa. Palibe njira yotulukira mu izo, inu mudzafa. Ndipo motsimikiza basi pamene inu mukudya za Iwo, inu mudzakhala ndi moyo; palibe njira yotulukira mu izo, inu mukuyenera kukhala ndi moyo. Ameni! Ngati iwo umabereka imfa yeniyeni, Uwu umabala Moyo weniweni. Ndiyo njira yokhayo yomwe inu mungakhoze kulandirira izo, ndi kukhala ndi Moyo.

²³⁹ Tsopano, mneneri ananena, kuti, “Kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo.” Tsopano taonani. Iye anati padzakhala tsiku lomwe lidzakhale la chimbuuzi, silimadzatchedwa usana kapena usiku. Liri ngati la mitambo, la chifunga, tsiku lozizira, komabe Mwana akupereka Kuwala. Mmwamba mwa chifunga ndi mitambo ndi zina zotero, Mwana akupereka Kuwala. Izo zimapereka Kuwala kokwanira inu mukhoza kuyendamo, ndipo inu mukhoza kuwona momwe mungayendere, ndi zina zotero, komabe ilo—ilo si lowala, tsiku lokongola. Mukuona? Tsopano, palibe nkomwe chomwe chingakhale moyo mu tsiku limenelo.

²⁴⁰ Ngati inu mungabzale chirichonse komwe dzuwa silikumanya izo, izo zimapinimbira. Si kulondola kumeneko? Inu alimi mukudziwa zimenezo. Mukaika chimanga mu mthunzi kapena penapake, mupenye, zimanyalitsa icho. Fred, iwe uyenera kudziwa zimenezo ndi tirigu wako. Inu mukakaiyika iyo kumeneko, ndipo ngati muli ndi chirimwe choyipa, oh, kozizira ndi mvula, iyo imanyala.

²⁴¹ Chabwino, ndiro limene liri vuto ndi mpingo kudutsa mibadwo iyi, iwo wanyalitsidwa. Iwo wanyalitsidwa ndi zipembedzo, “Kuika dzina lanu pa bukhu. Ife tinali nako Kuwala kokwanira kuti tidziwe kuti kuli Mulungu.” Ndine wokondwa ndi zimenezo. “Ife tinakhala ndi Kuwala kokwanira kuti tidziwe kuti kuli Khristu, kuli chiweruzo chimene chikubwera. Ife tinakhala nako Kuwala; chotero ife tinayika maina athu pa mabukhu, ife tinagwirana chanza ndi abusa, zina zotero, ndipo tinachita zimenezo.” Chabwino, koma tsopano ndi nthawi ya kumadzulo.

²⁴² Tsopano, chitukuko chabwera kuchokera kummawa mpaka kumadzulo, ndipo tsopano ife tiri ku Gombe Lakumadzulo. Ife sitingapitirirensa patsogolo; ife tawoloka, ife tabwerera Kummawa kachiwiri. Ife sitingapitirirensa patsogolo, ife tiri ku Gombe Lakumadzulo.

²⁴³ Tsopano, Baibulo linati, “Mu nthawi Yakumadzulo Kuwala kudzafika.” Tsopano, ndi mtundu wanji wa dzuwa limene limawala mu nthawi ya kumadzulo? Kodi ndi dzuwa losiyana ndi lomwe limatuluka mmawa? Ndi dzuwa lomwe lomwelo. Nkulondola uko? Chabwino, ndiye, kodi Mulungu analonjeza chiyani? Tsopano ife tifika kwa izi, tigwire izo, pansu pomwe apa pa m’badwo *uno*. Baibulo linanena chomwecho, ine nditsimikizira izo, mibadwo ya mpingo iyi, pamene ife tikupitirira, kuti, “Mu nthawi ya kumadzulo kudzabwera Kuwala kumene kudzatulukire Kumadzulo komwe kuti kudzabwezeretse Dzuwa la Chirungamo kachiwiri ndi machiritso mmapiko Ake. Ndipo zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa zomwezo zomwe zinkachitika kumbuyo kuno Kummawa zidzachitidwa cha kuno Kumadzulo, ndi kutsanulira kwina kwa Mzimu Woyera mu tsiku lotsiriza.”

Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo,
 Njira ya ku Ulemerero inu ndithudi
 mudzaipeza;
 Mu njira yamadzi imeneyo, Ndiko Kuwala lero,
 Kumizidwa mu Dzina lofunika la Yesu.
 Ana ndi aakulu, lapani machimo anu onse,
 Mzimu Woyera ndithu udzalowamo;
 Kuwala kwa madzulo kwabwera,
 Ndi zoonza kuti Mulungu ndi Khristu ali
 Mmodzi.

Oh, kudzakhala Kuwala nthawi yamadzulo,
 Njira yopita ku Ulemelero ndithudi
 mudzaipeza;
 Mu njira yamadzi iyi ndi Kuwala lero,
 Kumizidwa mu Dzina lofunika la Yesu.
 Ana ndi aakulu, lapani machimo anu onse,
 Mzimu Woyera ndithudi udzalowamo;
 Kuwala kwamadzulo kumeneko kwabwera,

244 Chinthu chomwecho chimene Petro ananena, “Mulole zidziwike kwa inu, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyo, amene inu munampachika, zonse Ambuye ndi Khristu. Lapani, wina aliyense wa inu” iye anatero, “ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu.”

245 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Monga ine ndinali kuyankhulira tsiku lina za *malangizo a kamwedwe a adokotala*. Anthu samakonda kutsatira malangizo a kamwedwe a adokotala. Ngati iye ali ndi—mankhwala omwe angachiritse matenda ako, ndipo iwe nkulepheranso. . . iwe nkukana kuti umwe iwo, ilo si vuto la adokotala kuti iwe umwalira. Ayi, bwana. Ilo ndi vuto lako, chifukwa iwe wakana kuwamwa iwo.

246 Ndipo tsopano, ngati adokotala alemba malangizo a kamwedwe ndipo iye. . . ndipo iwe nkutengera malangizo a kamwedwe amenewo kupita nawo kwa dokotala wabodza, ndipo iye nkuika chinachake mmenemo chimene sichikuyenera kukhala mmenemo, icho chingakuphe iwe, aponso. Nkulondola uko? Dokotala ameneyo anaphunzira zimenezo mpaka iye amadziwa kuti pali malangizo akamwedwe amenewo ochuluka kwambiri omwe amakhala chiphe, kupha msikidzi zimenezo zomwe ziri mthupi lanu; ndipo muli katemera wokwanira mmenemo wokhoza kusokoneza chiphe kuti icho chisakupheni inu. Ndipo izo ziyenera kukhala pa mulingo. Ngati inu muyika katemera wochuluka kwambiri, izo sizingamuthandize wodwalayo; mukaika chiphe chochuluka kwambiri, icho chidzamupha iye. Izo ziyenera kukhala pa mulingo.

247 Funso linali, “Kodi kulibeko mvunguti ku Gileadi? Kodi kulibeko asing’anga kumeneko?” anatero mneneri. “Ndiye nchifukwa chiyani matenda a mwana Wanga wamkazi sakuchiritsidwa.” Chavuta ndi chiyani ndi mpingo? Chavuta

ndi chiyani kuti tiri ndi matchalitchi ambiri odwala? Chifukwa takhala tiri ndi azamankhwala ena abodza amene amapereka Malangizo a kamwedwe molakwika. Ndiko kulondola. Iye sananene konse, “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Iye . . .

²⁴⁸ Kodi Malangizo a kamwedwewo anati chiyani? Apa pali Petro. Ndi angati akudziwa kuti iye anali ndi mafungulo aku Ufumu? Yesu ananena chomwecho. Kodi Iye ananena chiyani? Mwakuyankhula kwina, iye ali ndi cholemba cha inki cha Malangizo a kamwedwe.

²⁴⁹ Pamene iwo anamva izi zonse zikufalitsidwaponse, (Iwo anali akukuwa, akufuula, akuyankhula mmalirime, ndi kumakhala ndi nthawi yoteroyo.) ndipo iwo anati, “Anthu awa akhuta vinyo watsopano.”

²⁵⁰ Petro anati, “Awa sanakhute vinyo watsopano, monga mmene inu mukuganizira, powona kuti ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi chijachi chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli, ‘Izo zidzachitika mu tsiku lotsiriza,’ atero Mulungu, ‘Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse. Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera, ndi pa adzakazi anga ndi antchito anga Ine ndidzatsanulira za Mzimu Wanga, ndipo iwo adzanenera. Ndipo ine ndidzawonetsera zizindikiro mmiyamba kumwamba, ndi kupansi; moto, ndi utsi, ndi nthunzi. Ndipo kudzachitika kuti yense amene adzaitana pa Dzina la Ambuye sadzatero . . . adzapulumutsidwa.’”

²⁵¹ Ndipo komanso iye ananena zokhudza Davide, iye anati, “Mbadwa Davide anaziwoneratu izo, ndipo iye anati, ‘Kuwonjezera apo mnofu wanga udzapuma mu chiyembekezo chifukwa Iye sadzawusiya moyo Wanga ku gehena, komanso Iye sadzalola Woyera Wake Uyo kuti awone chivundi.’ Ndiroleni ine ndiyankhule nanu momasuka, abale, za mbadwa Davide, iye anamwalira ndipo anaikidwa mmanda, ndipo manda ake ali ndi ife mpaka lero. Mwawona, koma iye, pokhala mneneri, anawona chiwukitsiro cha Khristu. Mulole izo zidziwike kwa inu, kuti Yesu uyu, amene inu munampachika ndi manja awuthakati, Mulungu wamupanga Iye kukhala zonse Ambuye ndi Khristu.”

²⁵² Pamene iwo anamva izi, iwo analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati, “Amuna ndi abale,” kapena, “Dokotala Simon Petro, tilembereni ife Malangizo a kamwedwe. Kodi ife tizichita motani Izi? Ife tikufuna mankhwala a tchimo.” Oh!

²⁵³ Tsopano mpenyeni iye, zomwe iye ananena. Tsopano inu mupeza kumene mipingo iyi inachoka panjira. Iye anati, “Dikirani miniti! Ine ndilemba Malangizo a kamwedwe, ndipo iwo adzakhala Malangizo a kamwedwe a Muyaya. Iwo adzakhala a kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ndi ngakhale ochuluka omwe Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

254 Kodi iye anati chiyani? Iye anakonza motani izo? Monga Akatolika amachitira izo? Monga Abaptisti amachitira izo? Monga Amethodisti amachitira izo? Mmodzi aliyense wa iwo wawonjezera chinachake kapena wachotsapo chinachake kwa Iwo. Monga Achipentekoste? Iwo anawonjezera kapena anachotsapo. Koma kodi iye ananena chiyani? “Lapani, wina aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalondira mphatso ya Mzimu Woyera.” Malangizo a kamwedwe a Muyaya! “Ndi a inu, ndi a ana anu; izi zidzakhala za mpaka mu mibadwo yonse ya mpingo, aperekeni Iwo kwa aliyense wa iwo.”

255 O Mulungu, yeretsani manja anga. Yeretsani mtima wanga, Ambuye. Mulole... Ngati izo zingatengere mzanga aliyense yemwe ine ndiri naye, mudirole ine ndipereke Malangizo a kamwedwe momwe Adokotala anati ndiziperekerana Iwo.

256 Ndi chifukwa chake inu muli ndi mipingo yambiri yakufa, mamembala ambiri akufa. Inu mukuwonjezera katemerayo, ndipo mukuchotsa zambiri pa Iwo mpaka Malangizo a kamwedwewo sali mmene akuyenera kukhalira nkomwe, iwo sangachiritse nkomwe chirichonse; kugwirana chanza, ndi kujowina matchalitchi, ndi kukonkha. Oh, chifundo, zimenezo si Malangizo a kamwedwe, izo ndi imfa. Ngati inu mukufuna Moyo, ndipo mukufuna Mzimu Woyera, mutsatire zimene Mulungu anati muzichita. Mutenge Malangizo a kamwedwe! Ndizo ndendende momwe Iye ananenera, “Musamawonjezera kwa Iwo kapena kuchotsera kwa Iwo.” Ndiye apa pakubwera Chivumbulutso pomwepo ndipo akuti, “Aliyense amene adzachotsera kapena kuwonjezera, yemweyo adzachotsedwa (gawo lake) kuchoka mu Bukhu la Moyo.” Oh, mai, ameneyo ndiye Dokotala *wamkulu*. Oh, ine ndimamkonda Iye. Si choncho inu?

257 Oh, kwa m'badwo wawukulu uja, wa M'badwo wa Efeso, pamene mpatuko uwu unangoyamba kulowa mkati, kuti ukapange mabungwe. Ndipo azibusa ndi madikoni... kapena osati madikoni, koma abusa... osati azibusa, koma Makardinolo, mabishopu, mapapa, oyang'anira mpingo, kumawuza Mzimu Woyera, kumawuza Mpingo, “Tsopano, inu simungakhale nazo izo muno!” Bwana ndi ndani, mulimonse?

258 Petro anafunsidwa zimenezo nthawi ina. Anati, “Inu simungalalikirenso mu Dzina la Yesu. Inu mutha kulalikirana ngati inu mukufuna kutero, koma osati mu Dzina la Yesu.” Oh, mdierekezi amadana nalo Dzina limenelo!

259 Petro anati, “Kodi ndi zoyenera kwa ine kuti...” Baibulo linati, “Petro atadzazidwa ndi...” (chipembedzo?) Oh, aha, “. . . Mzimu Woyera.” Anati, “Dikirani, ine ndipita ndikamuwone woyang'anira wamkulu, kuti ndikawone zimene iye angandiuze ine kuti ndizichita pa Izi.”

260 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Kodi inu mumadziwa kuti a Assemblies of God ali ndi wowapima ubongo woti aziwaweruza, ndi kupita kukatenga amishonare awo kupita nawo kwa wowapima ubongo, kuti akawone ngati munthu ameneyo ali wokhoza kukhala wamishonare? Pentecostal Assemblies of God. Ndi angati amene anayamba amvapo zimenezo? Ndithudi, ziri paliponse, aliyense amazidziwa. Ndithudi. Nndani woti azimuyang'anira mmishonare ndi kukhala woweruza, wopima ubongo kapena Mzimu Woyera? Onani, ndi zomwe inu mumapeza, pokhala ndi munthu. Mwaona, mfundo zopangidwa ndi anthu, ziphunzitsa zopangidwa ndi anthu. Mudikire mpaka ife tidzafike ku m'badwo wa Pentekoste umenewo! Mulungu adzachiwotcha chinthu chimenecho motsimikiza basi monga dziko. Inde, bwana. Inde, ndithudi. Ndipo inu mudzawona chikuyaka moto njira yonse mpaka pansu. Uh, hum. Ndendende.

261 Koma tsiku lina laulemelero Iye adzabwera. Ndipo kumbukirani, mveterani, pali mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Nkulondola uko? Pali mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Ndipo inu mukukumbukira pamene iwo anatulukira kuti akakomane ndi Mkwatibwi—Mkwati, ena anagona tulo mu ulonda woyamba (Nkulondola uko?), ulonda wachiwiri, (Ndithudi, osati—osati anafa, anagona tulo.) ulonda wachitatu, wachinai, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi; ndipo mu ulonda wachisanu ndi chiwiri kunamveka mfuwu, “Taonani, Mkwati akubwera! Pitani uko mukakumane naye Iye!” Chinachitika ndi chiyani? Anamwali onse aja amene anagona, anauka.

Mmawa wowala wopanda mitambo pamene akufa mwa Khristu adzawuka, (Wopanda mitambo, Kuwala kwamadzulo kudzakhala kukuwala.)

Ndipo mmawa udzafika ku Muyaya, kowala ndi kokongola;

Pamene opulumutsidwa padziko lapansi adzasonkhana mnyumba zawo kuseri kwa thambo,

Pakuitana, ndidzakhala komweko.

Pakuitana dzina langa,

Pakuitana dzina langa,

Pakuitana dzina langa,

Pakuitana dzina langa, ndidzakhala komweko.

Tiyeni timgwirire ntchito Mbuye kuyambira

mbandakucha mpaka kulowa kwa dzuwa,

Tiyeni tiyankhule za chikondi ndi chisamaliro

Chake chonse chodabwitsa;

Ndiye pomwe moyo ukadzatha, ndipo ntchito

yathu idzathanso,

Pakuitana dzina langa, . . .

Mwana aliyense wa Mulungu kwezani manja anu tsopano:

Pakuitana dzina langa,
 Pakuitana dzina langa,
 Pakuitana dzina langa,
 Pakuitana dzina langa, ine ndidzakhala
 komweko. (Oh!)

Bwinoli tipita,
 Tidzacakomana pa Gombe lokongola lija;
 Bwinoli tipita,
 Tidzacakomana pa Gombe lokongola lija.

262 Kodi mumazikonda nyimbo zakale za tchalitchi? Oh!

Kwa Atate athu achifundo mmwamba,
 Ife tidzakupereka mtulo wathu wa
 kupembedza,
 Kwa mphatso ya ulemelero ya chikondi Chake,
 Ndi madalitso omwe amayeretsa tsiku lathu.

Bwinoli tipita,
 Tidzacakomana pa Gombe lokongola lija;
 Bwinoli tipita,
 Tidzacakomana pa Gombe lokongola lija.

Tsopano gwiranani chanza ndi winawake yemwe
 wakuzungulirani, pozunguliraponse monga choncho.
 Ndizabwino zimenezo.

. . . bwinoli tipita,

Nenani, "Ine ndidzakumana nanu m'bale."

Tidzacakomana pagombe lokongola lija;
 Bwinoli tipita,
 Tidzacakomana pa Gombe lokongola lija.
 Tidzakaimba pa Gombe lokongola lija,
 Nyimbo yokoma . . .

Aliyense ayimbe iyo tsopano.

Ndipo mzimu wathu sudzakhalanso
 wachisoni,
 Osadandaula chifukwa chamadalitso athu
 ampumulo.

Aliyense, ndi manja anu mmwamba:

Mu bwinoli tipita,
 Oh, tidzacakomana pa Gombe lokongola lija;
 Bwinoli tipita,
 Tidzacakomana pa Gombe lokongola lija.

263 Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano, tiyeni tinene izi:

Ambuye Yesu, Ine ndimakukondani inu. Ine
 ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu,
 Mulungu wowonetseredwa mu thupi kuti adzachotse tchimo
 langa. Ine sindimadalira kukhoza kwanga, Ine ndiribe
 kulikonse, koma ine mwaulemu ndikudalira mu kukhoza kwa

Yesu Khristu amene ali Mpulumutsi wanga, Mulungu wanga, Mfumu yanga. Ine ndimamukonda Iye. Amen.

²⁶⁴ Mawa usiku seveni koloko, Ambuye akalola, ife tidzatenga mpingo wa Smurna.

Bwinoli . . .

Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano.

(Oh, tipita!)

Tidzakakomana pagombe lokongola lija;

(Bwinoli!)

Bwinoli tipita,

Tidzakakomana pa Gombe lokongola lija.

Tsopano mofewa, aliyense, mokoma:

Oh, kwa Atate athu achifundo akumwamba,

Ife tidzakupereka mtulo wathu wa

kupembedza,

Chifukwa cha mphatso yaulemelero ya

chikondi Chake . . .



M'BADWO WA MPINGO WA EFESO CHA60-1205
(The Ephesian Church Age)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lolemba madzulo, Disembala 5, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2022 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org